

# UMODZI



Zikomo inu, M'bale Orman. Ambuye akudalitseni inu.

Mmawa wabwino, abwenzi. Ndi zabwino kukhala kuno mu kachisi kachiwiri mmawa uno. Ndipo ndinangoyima kumbuyo uko kumamvetsera, pamene ine ndimalowa, ndi kumamva uneneri ukupita mwanjira ya kuyankhula mmalirime, ndi kutanthauzira. Ndipo ine ndinanena kwa anthuwo kuti chipindacho chadzaza nachonso, chotero ine ndinati, “Ine sindikudziwa, ine sindinayankhule naye munthu uyu” (Ameneyo anali M'bale Higginbotham, ngati ndalondola za munthuyo.) “kwa nthawi yaitali. Yakhala ili miyezi chigwirireni dzanja lake.” Koma ndizo ndendende zomwe ine ndikuyankhulapo, zimene iye ananena mmawa uno, ndendende zomwe ine ndikuyankhulapo. Iye samadziwa izo. Ine sindimadziwa izo inemwini mpaka kanthawi kapitako, chimene ine ndimati ndiyankhulepo. Ndipo ndizo basi, zomwe iye ananena nthawi imeneyo. Chotero ife tiri okondwa kudziwa kuti ife tasonkhana mu Dzina la Ambuye Yesu, ndipo pansi pa mapiko Ake otezeza.

<sup>2</sup> Tsopano, ine ndikuwona ambiri ayimirira, malo adzaza ndi kuchulukana, ndipo ife timangodana nazo kuti tiziwona zimenezi. Ndipo, mwamsanga momwe ife tingathere, ife tizipanga izo mosiyana pano, kachisi wokulirapo. Tsopano, ine ndikufuna kuti ndilengeze zaku Phoenix mwamsanga basi.

<sup>3</sup> Ine ndinali pano Lamlungu lapitali usiku ndipo ndinayankhula pa phunziro la *Mgonero* kwa a...usanayambe utumiki wa mgonero. Mgonero sikudya mkate, *commune* amatanthauza “kuyankhulana, kuyankhula mobwezera, kuyankhula ndi winawake.”

<sup>4</sup> Ndipo tsopano mmawa uno, ngati ine ndingatenge nthawi yaitali kwambiri, bwanji, winawake asinthane mipando ndi iwo amene ayimirira, ndipo izo ziyamikiridwa, muwalole iwo akhale pansu pang'ono pokha. Ine—ine ndikukhudzidwa ndi nthawi ino imene tikukhalamo. Ndimakhala kwambiri, wokhudzidwa kwambiri. Pamene ndiwona zinthu zikuchitika zomwe ine ndikuziwona zikuchitika, pali chinachake mkati mwanga chimene chimakondowezeka. Ndipo ine ndikufuna kuti ndingotenga nthawi yanga ndikuyesera kuti . . .

<sup>5</sup> Uthenga wa mmawa uno ndikuyankhula pa phunziro la *Umodzi*. Ndipo ine—ine ndikufuna kuti nditenge nthawi yanga ndi kuyesera kuzipanga izo basi momwe...kuziika izo mwangwiro basi monga ine ndikudziwira. Ndipo ndikukhumba mapemphero anu pamene mwasonkhana.

<sup>6</sup> Ndipo tsopano ine ndikufuna kuti inu mutsegule, ngati inu muli ndi Baibulo ndipo mukufuna kuti muwerenge

ndi ine, ku mutu wa 1 wa Ahebri, poyamba. Ndipo ine ndikufuna kuti ndiwerenge ndime zitatu zoyambirira za mutu wa 1 wa Ahebri, ndipo kenako Genesis 1:26 ndi 7, kuti ndizimangirize izo pamodzi. Ndipo palibe munthu amene anganene chirichonse chimene chiri choyenera kunena pokhapokha Mulungu atamuthandiza kunena icho. Ndipo—ndipo izo ziri motsatira Uthenga mmawa uno, nawonso, wa umodzi wa anthu ndi Mulungu. Tsopano mu Ahebri mutu wa 1, ife tikuwerenga izi.

*Mulungu, amene mu nthawi zakale...mu njira zosiyanasiyana ankayankhula nthawi zakale kwa makolo mwa aneneri,*

*Mmasiku otsiriza ano wayankhula kwa ife kudzera mwa wake...mwa Mwana wake, amene iye wamusankha kukhala wolowa mmalo wa zinthu zonse, mwa ameneyonso iye anapanga mayiko;*

*Amene pokhala mu mawalitsidwe a ulemelero wake, ndi chifanizo chofotokozedwa cha umunthu wake, ndi kunyamula zinthu zonse ndi mawu a mphamvu yake, pamene iye mwa yekha anayeretsa machimo athu, anakhala pansi pa dzanja lamanja la Ukulu mmwamba;*

<sup>7</sup> Ndipo tsopano mu Genesis, a—mutu wa 1 ndi ndime ya 27, 26 ndi 27, ine ndikuwerenga izi.

*Ndipo Mulungu anati, Tiyeni ife tipange munthu mu chifanizo chathu, mwa mafanizidwe athu: ndi kulola iwo akhale ndi ulamuliro pa nsomba za m'nyanja, ndi pa mbalame za mmlengalenga, ndi pa ng'ombe, ndi pa dziko lonse lapansi, ndi pa zokwawa zonse zomwe zimakwawa pa dziko lapansi.*

*Chotero Mulungu analenga munthu mu chifanizo chake chomwe, mu chifanizo cha Mulungu anamulenga iye; mwamuna ndi mkazi iye anawalenga iwo.*

<sup>8</sup> Tsopano tiyeni tiweramitse mitu yathu mphindi yokha pamene ife tikupemphera. Ndipo ndikutsimikiza kuti pali zopempha zambiri mwa omvetsera ochuluka chotere, chotero mwinamwake ife tingokweza dzanja lathu kwa Mulungu, amene ali ndi chopempha, ndipo mulole iye mwa ichi achipange kudziwika kuti ife tiri ndi chinachake chimene ife tikufunira pemphero. Mulungu apereke kwa aliynense wa inu.

<sup>9</sup> Ambuye, ife tasonkhana pansi pa denga la kachisi uyu, ndipo tiri othokoza kukhala ndi denga pa ife lero, koma kubwera kwathu pamodzi kunali kwa cholinga chachikulu kuposa ichi. Ife tikumverera kuti mwa lonjezo la Mulungu tasonkhana pansi pa mapiko a Wamphamvuzonse. Kutu Iye, monga nkhuu ingaphimbire anapiye ake, atitetezere ife ku zonse zomwe tikufuna kuti Iye atiteteze kwa izo. Kutu Iye afungatire pamwamba pa ife ndi kutidyetsa ndi kutipatsa ife

lero mkate wathu wa tsiku ndi tsiku, zonse ziwiri mwathupi ndi mwauzimu, kuti tikhoze kukhala nayo mphamvu yolimbikitsa ya thupi kuti tiziyendayenda padziko lapansi, ndi mphamvu yolimbikitsa ya Mzimu Woyera kuti ibweretse Mawu a Mulungu kwa anthu anjala. Ndi kuchoka pano ndi Iwo pa milomo yathu ndi mmitima yathu, ndi Mafuta odzodza atsopano otero kuti tikakhoze kukawauza ena za tsiku lomwe ife tikukhalamo, ndi chikholidwe cha nthawi. Mulungu, ife tikudalira kwathunthu mwa Inu. Palibe malo ena atsalira amene aliyense angapiteko. Ife tikumverera monga mmene Petro anamverera, tsiku lija pamene Yesu anati, “Kodi inunso mupita?”

<sup>10</sup> Iye anati, “Ambuye, ife tipitanso kuti? Inu nokha muli ndi Mawu a Moyo Wamuyaya.” Ndipo ndi chifukwa chake ife tasonkhana mu Dzina Lanu mmawa uno, chifukwa Inu nokha muli nawo Mawu a Moyo Wamuyaya. Ndipo ife tikupemphera kuti Inu mupange ichi chenicheni kwa aliyense wa ife lero kuti mitima yathu itenthe mkati mwathu. Miyoyo yathu ilimbikitsidwe, matupi athu achiritsidwe, mizimu yathu ichiritsidwe, miyoyo yathu ikonzedwe kukhala yatsopano, kulengedwa monga momwe Mulungu akanatifunira ife.

<sup>11</sup> Atate, ine ndikupemphera kuti Inu mupereke mphamvu kwa iwo amene ayima mu zipinda ndi kuzungulira makoma, ndi pakhonde mozungulira. Ine ndikupemphera kuti Inu muwapatse iwo mphamvu. Ndipo, podziwa izi zikupita pa tepi, zimene ziti zipite ku mafuko ambiri osiyanasiyana, kunja uko mmayiko ndi mafuko a dziko lapansi. Ndipo, Mulungu, ife tikudalira kwathunthu mwa Inu. Mungotipatsa ife mphamvu ndi—Mawu ndi kudzodza, kuti izo zikhale basi momwe Inu mungakhalire nazo izo kwa ora lino. Ife tikudzipeka tokha kwa Inu tsopano, kumvetsera kwathu, liwu lathu, chidwi chathu, zonse zomwe ife tiri, ife tikuzipeka kwa Inu, kuti Inu musunthe mwa ife. Gwirani ntchito kupyolera mwa ife ndipo muwonetsere Kukhalapo Kwanu kwakukulu ndi ife. Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu, Mwana Wanu. Amen.

<sup>12</sup> Mawu akuti *umodzi* amatanthauza “kukhala mmodzi naye.” *Umodzi*, “kugwirizana.” Ndipo, tsopano, ili ndi phunziro ndithu, ndipo ilo—ilo likuyenera tcheru chochuluka kuposa momwe ndingathere kupereka ilo, ndipo kuposa momwe munthu aliyense padziko lapansi angaperekere. Koma ine ndikufuna kuti ndifotokoze kwa inu lingaliro langa la izo, ndi, ndi chimene Mulungu ati atipatse ife. Tsopano, mu ichi, ndi kuphunzitsa chiphunzitsa. Ndipo kwa abale amene adzamvetsera tepi iyi, ine ndikudalira kuti iyo siyidzakhala chokhumudwitsa, koma iyo idzakhala kuti ikupangitseni kuti muzitenge izi molingalira kwambiri, pansu pa kulingalira, kani. Kutu muziphunzire izo mwapemphero, mosamalitsa, ndi kuziyeza izo mu muyezo wa Mawu a Mulungu, kuti muwone ngati Iwo ali a Mulungu kapena ayi.

<sup>13</sup> Pakuti ine ndikukhulupirira kuti umo ndi momwe ife tikuyenera kumachitira nthawizonse, kuziyeza zinthu ndi Mawu, chifukwa Mawu ndi Chinthu chokhacho chimene chiti chidzatsalire. Yesu anati, “Zonse kumwamba ndi dziko lapansi zidzachoka, koma Mawu Anga sadzachoka.” Ndi chifukwa chake ine ndimawakhulupirira Iwo, ndi kukhulupirira Iwo kukhala dongosolo la Mulungu. Ine ndikukhulupirira kuti Iwo ndi ntchito yotsirizidwa ya Mulungu yolembedwa mu Mawu. Chotero, kuti ngati chirichonse chikanakhala chosiyana ndi Mawu amenewo, icho sichikanakhala Mulungu kapena dongosolo la Mulungu. Ine ndikukhulupirira Iwo ndi dongosolo. Tsopano, Mzimu wa Mulungu mu Mawu umawapangitsa Mawu kukhala Okha, kudzipanga Okha. Iwo umabweretsa Mawu ku moyo, monga mbewu.

<sup>14</sup> Tsopano, munthu woyamba ndi mkazi woyamba m'munda wa Edeni anali mu mgwirizano wangwirowo ndi Mulungu, chotero kuti Mulungu ankakhoza kutsika panso nthawi iliyonse imene Iye akhumba ndi kuyankhula mlomo-ku-khutu ndi Adamu ndi Eva. Tsopano, uwo ndi umodzi wangwirowo, Mulungu ndi chirengedwe Chake, Mulungu akuyankhula mlomo-ku-khutu ndi Adamu ndi Eva. Ndipo iwo anali angwirowo kwambiri mu chiyanjano ndi Mulungu mpaka iwo anali mmodzi ndi Mulungu. Mulungu ndi banja Lake anali amodzi.

<sup>15</sup> Mwamuna aliyense ndi banja lake, banja lolondola, labwino, lolemekezeka, lomvera limakhala ndi wina ndi mzake, banja lirilonse. Ndipo ngati pakhalala chinachake m'banja chimene chikuwalekanitsa iwo, ndiye kuti izo si zabwino, banjalo lasweka penapake. Iwo onse azikhala mmodzi, bambo ndi mayi, mayi ndi bambo, ana ndi kholo, kholo ndi ana, onse kumagwirizana. Ndipo, pamene inu muchiwona icho, mudzawona chithunzi chimodzi chokondeka.

<sup>16</sup> Ndicho cholinga cha Mulungu. Ndipo cholinga Chake monga Atate, wamkulu, chinali choti adzakhale mmodzi ndi banja Lake, banja lapadziko lapansi, Adamu ndi Eva. Ndipo njira yokhayo imene iwo akanakhalira amodzi ndi banja, kapena ndi Mulungu, inali chifukwa chikhalidwe cha Mulungu chinali mwa iwo. Chotero izo zinawapanga iwo ndi chikhalidwe cha Mulungu mwa iwo, kenako ndi wina ndi mzake ndi Mulungu, iwo anadzakhala onse mmodzi. Kodi chimenecho si chithunzi chokongola, Mulungu mu banja Lake, Atate pa onse, wapamwamba! Kopanda imfa, kopanda chisoni, kopanda kupweteka kwa mtima, kopanda kanthu; basi chimwemwe chosaneneka; osakhalanso odwala, osakhala ndi kupweteka kwa mtima, kungokhala mmodzi ndi Mulungu! Ndi chithunzi chotani! Chifukwa, chikhalidwe chomwe cha Mulungu chinali mwa anthu awa. Ndipo chotero, chimene iwo ankachita, iwo ankatsatira basi mu mzere ndi Mulungu, ndipo Mulungu ndi iwo anawapanga iwo mmodzi.

17 Tsopano, Yesu anapemphera, mu Yohane, mutu wa 17 ndi ndime ya 11, kwa inu amene mumalemba mitu ya Sande sukulu iyi. Ine ndiri nayo yochuluka ya iyo mmawa uno. Yohane 17:11, Yesu anapemphera kuti Mpingo ndi Iye akhale mmodzi monga Iye ndi Atate anali Mmodzi. Kuti Mpingo, ife monga ziwalo za Thupi la Khristu, tidzakhale mmodzi, pamodzi, chimodzimodzi monga momwe Iye ndi Atate ali Mmodzi. Ndipo pa tsiku limenero ife tidzadziwa kuti Iye anali mwa Atate. . . Atate mwa Iye, ndipo Iye mwa ife, kuti pamodzi ife tinali mmodzi. Ndi mgwirizano wotani, umodzi umene udzakhale, kumuwona Mulungu mu Mpingo Wake mpaka membala aliyense nkumakhala mwangwiro basi mu chiyanjano wina ndi mzake ndi Mulungu. Ndiwo Mpingo umene Yesu akuwudzera. Ndi pamene pemphero Lake lidzayankhidwe, kuti ife tidzakhale mmodzi.

18 Ndipo ndi maziko okhawa a chiyanjano omwe Mulungu anayamba wadziyikirapo Iyemwini ndi Mpingo Wake, ndi umodzi wa Iyemwini mwa anthu. Ndiwo maziko okhawa a chiyanjano. Ndipo njira yokhayo yomwe inu mungakhalire ndi maziko amenewo ndi mwa chilumikizano, kuti mulumikizane ndi Iye kwanthawizonse. Chimodzimodzi monga pamene inu mwalumikizana ndi mwamuna wanu, mkazi kulumikizana ndi mwamuna wake, ndi lumbiriro la mpaka imfa. Tsopano, ndiye pamene inu mulumikizana ndi Mulungu, ndi chinthu chomwecho kuti mpingo unalumikizana ndi Khristu, ndi mpaka imfa idzatilekanitse. Ndiyeno ngati inu simudzachimwa kose kapena kuchita chirichonse cholakwika, inu mudzakhala olumikizidwa Mwamuyaya ndi Mulungu. Ndipo imfa yokha ingakuchotseni inu kwa Mulungu, ndipo osati imfa yathupi, koma tchimo la imfa. Tchimo ndi imfa, ndipo ilo limakuchotsani inu kwa Mulungu. Chotero, kulumikizidwa ndi Iye mu Mzimu wa mphamvu Yake, ndi Moyo Wamuyaya, inu ndi olumikizidwa Mwamuyaya ndi Mulungu. Oh, ine ndikufuna kuti ndifike kwa zimenezo pakapita kanthawi. Kulumikizana Kwamuyaya ndi Mulungu Wamuyaya, mwangwiro mu umodzi ndi Iye, kulumikizidwa pamodzi mwangwiro, Mpingo umene onse, awiri onse Mulungu ndi Mpingo Wake, ndi mmodzi, alumikizidwa pamodzi.

19 Ndipo ngati inu mungazindikire momwe Eva analumikizidwa ndi Adamu, iye anadzakhala gawo la iye. Mulungu, kodi inu munazindikira mu Genesis 1:27, Iye anamulenga munthu mwamuna ndi mkazi, Iye anawalenga iwo. Tsopano, munthuyo anali. . .awiri onse mwamuna ndi mkazi pamene izo zinafika pa kukhala mu mzimu wachikazi ndi wachimuna. Kenako Mulungu anatenga kumbali yake a—nthiti. Kodi inu munazindikira kuti gawo la thupilo linali chotulukapo, koma osati mzimu? Chiwalo cha thupi la mkazi chinali chotuluka, chirengedwe chitatsirizidwa kale, Mulungu

anatenga kuchokera kumbali ya Adamu nthiti ndipo anapanga mkazi. Koma osati mzimu, mzimu unali gawo la Adamu, pakuti iye anali ziwiri zonse mwamuna ndi mkazi, mka- . . . kuyankhula mwauzimu, ziwiri zonse mwamuna ndi mkazi.

<sup>20</sup> Tsopano, kodi inu simukuchiwona chithunzi chachikulucho? Ife, mu thupi, ndife osiyana. Tiri ngati chotulukapo, chinthu cholengedwa, mwa chikwati choyera. Koma mu Mzimu ndife ana aamuna ndi aakazi, osati mzimu wina, koma Mzimu wa Mulungu wamoyo. Ife tiri mu chifaniziro Chake, mu mgwirizano Wake, mu chifaniziro changwiwo cha Mulungu wamoyo, chifukwa ife timakhala ana aamuna ndi aakazi. Osati olekanitsidwa, koma Mzimu womwewo, Mulungu yemweyo, Munthu yemweyo, wolumikizidwa mu chikwati kwa Wamuyaya. Mukuona momwe Mulungu anazikonzera izo kuti ife tisakhale osiyana, koma Iye! Osati munthu wina wa fuko lina, koma chilumikizano chenicheni ndi mphukira ya Wamphamvuzonseyo, zochitika mwa kulumikizana koyera. Tsopano, thupi limachokera kwa amayi ndi abambo, koma Mzimu umachokera kwa Mulungu, Mulungu kudzigawaniza Yekha monga Adamu anagawanitsidwa.

<sup>21</sup> Pa Tsiku la Pentekoste, ife tikupeza Mzimu Woyera, Lawi la Moto, likudzigawaniza Lokha ndi kudzakhala pa membala aliyense wa Mpingo umenewo, Mulungu akudziika Yekha pamodzi! Kenako ndi gulu limenero la anthu pamodzi, kodi ilo limachita chiyani? Limabweretsa Thupi lolumikizana la Ambuye Yesu. Kubwera pamodzi!

<sup>22</sup> Ndipo lero mu kulekanitsidwa kwakukulu uku kumene ife tikukhalamo, kusiyana kwa zipembedzo ndi zinthu, zachisoni bwanji, ndi chamanyazi bwanji!

<sup>23</sup> Kulumikizana mu chikwati Chakumwamba kwa Mulungu Wamuyaya, gawo la Iye, gawo la Mulungu. Mu thupi ine ndinadzakhala Branham chifukwa cha abambo anga, a Branham. Inu mumakhala gawo la abambo anu ndi amanu, koma mu mzimu ife timakhala mu chilumikizano ndi Mulungu, ndi gawo la Mulungu. Ndicho chifukwa mzimu sungathe kufa. “Iye amene akhulupirira pa Ine ali nawo Moyo wosatha. Ndipo mu chifaniziro chimene iye ali pano pa dziko lapansi, ndi mu chifaniziro chake, Ine ndidzamuwukitsa iye mmasiku otsiriza.” Osati mzimu wokhalapo, pakuti ife tidzakhala nalo thupi monga thupi la ulemelero la Mulungu, thupi la ulemelero la Ambuye Yesu, lowukitsidwa mu Chifaniziro Chimenecho.

<sup>24</sup> Yesu anati, akupita ku manda a Lazaro, “Ndine chiwukitsiro ndi Moyo. Iye amene akhulupirira mwa Ine, angakhale iye atafa, komabe iye adzakhala moyo. Ndipo yense wakukhala moyo ndi kukhulupirira mwa Ine sadzafa konse. Khulupirirani *mwa* Ine, osati *pa* Ine, koma *mwa* Ine.” Kukhala *mwa* Iye, kukhulupirira! “Ngati mukhala mwa Ine ndipo Mawu

Anga mwa inu.” Mwa Iye, kukhulupirira! Oh, mai! Ine ndikuyembekeza Mzimu Woyera uzibweretsa izo kufika kwa inu. Tsopano, ndinu kagulu kakang’ono ka nkhosa, ndi chifukwa chake mu sabatayi, ndikupemphera ndi kumufunsa Mulungu, ndinasankha mutu uwu, kuti ndikuwonetseni inu pamene ife tayima. Kukhulupirira mwa Iye. Inu simungakhulupirire mwa Iye mpaka mutabwera mwa Iye, kapena, Iye atabwera mwa inu, zikatero inu mukukhulupirira mwa Iye, zikatero inu muli nawo Moyo Wamuyaya. Inu mukukhulupirira *pa* Iye mpaka inu mutalandira Moyo Wamuyaya, ndiye Moyo Wamuyaya ndi Moyo wa Mulungu mwa inu, ndiye inu mukukhulupirira *mwa* Iye.

<sup>25</sup> “Inu mwa Ine, Ine mwa inu. Kuti iwo akhale mmodzi, Atate, monga Inu ndi Ine ndi Mmodzi.” Mulungu mwa Khristu, Khristu mu Mpingo. Mukuona? “Monga ife tiri Mmodzi, chomwechonso iwo akhale mmodzi.” Ndiye mungakhale bwanji mmodzi? “Ngati inu mukhala mwa Ine, Mawu Anga mwa inu.” Mwaona, kukhala! “Mawu Anga mwa inu, ndiye pemphani chimene mukufuna.” Pakuti si inu aponso, ndi Mawu omwe ali mwa inu, ndipo Mawu ndi Mulungu.

<sup>26</sup> Tsopano, Mawu a Mulungu ndi Lupanga. Ahebri, mutu wa 4, amanena chomwecho, Ahebri 4:12. Tsopano, iwo ndi Lupanga. Ndipo lupanga limakhala matalala ngati silinaperekedwe ndi dzanja kapena mphamvu. Ndipo ilo...koma izo zimatengera dzanja kugwira Lupangalo. Ndipo zimatengera dzanja limene likugwira Lupanga ili, ndi dzanja la chikhulupiriro.

<sup>27</sup> Tsopano, dzanja limenelo la chikhulupiriro, zimatengera momwe mphamvu yake ikukhalira. Dzanja ili la chikhulupiriro likhoza kungokhala lamphamvu mokwanira kudula bowo laling’ono mundima ndi kuti, “Mwa chikhulupiriro ndapulumsidwa.” Ndiko kudula kwakukulu, koma, kenako, ngati ndizo mphamvu zonse zomwe dzanja limenero likunyamula Lupanga limenero, ndizo zonse zomwe ilo lingathe kudula. Koma, ngati ilo liri dzanja lamphamvu, ilo lidzadula kupyola chirichonse chimene mdierekezi angakhoze kuchiyika kunja uko, kupanga lonjezo lirilonse la Mulungu kuwala mu mphamvu ya chiwukitsiro Chake. Ngati ilo liri dzanja lamphamvu la chikhulupiriro, “Masiku a zozizwitsa! Yesu Khristu, yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawi zonse,” kudula njira yake kudutsa. Zimatengera mphamvu ya dzanja kumbuyo kwa Lupangalo.

<sup>28</sup> Ndipo Lupangalo ndi lakuthwa kwambiri. Ahebri 4, anati, “Ndi akuthwa kuposa lupanga lakuthwa konsekonse limene limadula ziwiri zonse zobwera ndinso zopita, ndipo limapita mpaka ku—mafuta a mmafupa, ndi molumikizira, ndi ozindikira malingaliro a mumtima.” Amapita kupyola chithupithupi, amapita mu gawo lauzimu ndipo amakatenga malingaliro a mumtima ndi kuwaulula iwo. Mzimu wa Mulungu, Mawu a Mulungu.

<sup>29</sup> Tsopano, Mawu amenewo adzadula mkati mmenemo ngati pali mphamvu yokwanira kumbuyo kwa Iwo kuti ikankhire Iwo mkati, iwo udzapeza malo Ake ndi kudula lonjezo lirilonse ndi kupereka Iwo kwa inu, ngati mutangokhala ndi nkono wamphamvu mokwanira kuseri kwa Iwo. Lupanga, linyamuleni Ilo mu nkono—nkono wa chikhulupiro! Ligwireni Ilo molimbitsa, mugwiritsitse pa Ilo ndi kuyenda mu nkhope ya mdani. Kodi mdani wosadulidwa ameneyo angayime bwanji mu Kukhalapo kwa Mulungu Wamuyaya? Chotero, inu mutenge Lupanga la Mawu, ndipo lonjezo lirilonse ndi lanu. Linyamuleni Ilo mu dzanja lamphamvu la chikhulupiro, muyende chitsogolo! Ngati inu mukufuna machiritso, aduleni iwo ndi Mawu, “Yesu Khristu, yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.” Ngati inu mukufuna chipulumutso, lonjezo lirilonse la mu Baibulo ndi lanu. Ilo liri kumbuyo uko ndipo Satana akuyesetsa kulibisa ilo, koma tengani Lupanga ndipo mukankhe kudutsa mumdima mpaka Kuwala kwa Mulungu kutawalira pa solo yanu ndipo inu nkukhala ndi lonjezo. Iye adzachita zimenezo.

<sup>30</sup> Adamu anali gawo la, kapena, Eva anali gawo la Adamu, iye anali mnofu wa mnofu wake ndi fupa la fupa lake. Ndipo ndicho chimene chilumikizano cholondola chiri. Ndipo ndicho chimene chilumikizano cholondola cha Mpingo chiri, Mzimu wa Mzimu Wake, Mawu a Mawu Ake. Osapatuka konse ku Mawu, wokhulupirira weniweni woona sadzalekelera pa Mawu aliwonse. Kumbukirani, anali Mawu amodzi okha amene Eva analekelerapo, Mawu amodzi. Koma wokhulupirira woona sadzalekerera pa Mawu aliwonse. Iwo adzagwira Lupanga la Chikhulupiro...mu chikhulupiro, kani, Lupanga la Mawu, ndi kutenga lonjezo Lauzimu lirilonse limene Mulungu anapanga. Ndi zimenezotu.

<sup>31</sup> Iwo anali zitsanzo za Mulungu kwa ife, chimene ife tikuyenera kukhala, iwo, opezekapo nthawizonse, osalephera konse. Pamene iwo alankhula, Mulungu ankayankha. Iye ankawayang’ana iwo, tsiku ndi tsiku. Usiku, pamene agona tulo, Iye ankawayang’anira iwo. Masana, Iye ankawatsogolera iwo, anawadyetsa iwo, ankawakonda iwo, ankayanjana nawo iwo mosalekeza, nthawi zonse. Iwo anali mu chifaniziro cha Mulungu, ndipo Mulungu amakhala mwa iwo. Icho ndi chimene chimapanga chiyanjano. Ndicho chimene chimapanga chilumikizano, ndi Mulungu kukhala mu Mpingo Wake. Ndicho chilumikizano. Zambiri zikhoza kunenedwa, ndiri ndi malo ambiri oti ndipiteko. Kulumikizana ndi Iye, ndi Moyo Wamuyaya. Ndipo njira yokhayo imene ife tingakhoze kulumikizana ndi Iye ndi kudzakhala gawo lirilonse la Mawu Ake. Uko nkulondola, kutenga lonjezo lirilonse ndi kulikhulupirira Ilo.

<sup>32</sup> Tsopano, Eva analumikizidwa kufikira iye ataswa Mawu



amodzi, kapena, atakayikira Mawu amodzi kukhala owona. Izo zinamulekanitsa iye. Mawu aliwonse, “Munthu sadzakhala moyo ndi mkate wokha, koma ndi Mawu aliwonse!” Chotero ife tikhoza kukhala mwa Mulungu, olumikizana, chifukwa Adamu ndi Eva, kugwa kusanachitike, kusakhulupirira kwa Mawu kusanachitike, anali chitsanzo cha zomwe ife tingakhale mwa Iye. Kulumikizidwa ndi Iye, ndi Moyo; kulekanitsidwa kwa Iye, ndi imfa. Tsopano, ngati ife titsatira malamulo Ake!

<sup>33</sup> Ife tikudziwa kuti timalakwitsa, koma inu musamayang’ane pa zimenezo. Si zolakwitsa zanu, chifukwa inu mudzakhala nazo izo nthawizonse. Koma, inu mukuwona, ndi kutsatira malamulo Ake, kutsatira zimene Iye anati tizichita. Kupunthwa ndi kugwa ziribe kanthu kochita ndi izo. Wantchito weniweni woona, ngati angapunthwe, iye adzadzukanso. Ngati iye agwedezeka, Mulungu amamukokeranso iye mu njira, bola ngati ali mu njira ya ntchito. Koma ngati iye wachoka pa njira ya ntchito, Mulungu samakhala wokakamizika kwa iye. Koma bola ngati iye ali mu njira ya ntchito, Mulungu amakhala wokakamizidwira kwa iye, podziwa kuti iye ndi mwamuna chabe kapena mkazi. Iye amakhala wokakamizidwa kwa munthu ameneyo bola ngati iwo ali mnjira ya ntchito.

<sup>34</sup> Tsopano, Mpingo tsopano watomeredwa kwa Khristu ku ukwati. Ukwatiwo siunachitikebe, iwo udzakhala pa Mgonero wa Chikwati cha Mwanawankhosa. Chotero, ife tikuwona kuti Mpingo tsopano watomeredwa, monga mwamuna kutomeredwa kwa mkazi wake. Kodi iye amachita chiyani pamene iwo atomeredwa? Iye amangopereka zinthu zamtundu uliwonse, kumutumizira iye mphatso, kumupangitsa iye kuti amverere bwino. Chabwino, ndicho chimene Khristu akuchita kwa Mpingo Wake. Iye akutitumizira ife mphatso za Mzimu. Kodi iwe ungakhale bwanji wotomeredwa pamene iwe ukukana kuti mphatso izi ziripo? Ndizo zizindikiro kumene zachikondi. Ndi chizindikiro cha Mulungu kwa Mpingo. Yesu ananena chomwecho, “Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira.”

<sup>35</sup> Tsopano, musunge zinthu zimenezo mmalingaliro. Mpingo ukuyenera kukhulupirira Mawu aliwonse, lonjezo lirilonse, gawo lirilonse, ndi kudzitengera Iwo kwa iwoeni, ndi kuchitachita okha mwa Iwo. Ngati ine ndinali wotomeredwa kwa mtsikana, ndipo ine ndinali mwamuna wosakwatira, ndipo nkutumizira iye chinachake, mphete ya chinkhoswe, ndipo iye osayivala iyo, ndiye izo zisonyeza kuti iye sakundikhulupirira ine. Iye—iye—iye sakufuna kukhala mkwatibwi wanga. Ndipo ngati Khristu awutumizira mpingo Wake mphatso zimene Iye analonjeza, ndipo iwo nkuzikana izo ndi kunena “izo siziri chomwecho,” iwo sakufuna kukhala Mkwatibwi wa Khristu. Iwo ndi opalidwa ubwenzi kwa wokonedwa wina, ndipo osati kwa Khristu, Mkwatiyo. Chotero Mpingo weniweni umasunga

lonjezo, ndi kusunga zonse, ndi kuvomereza mphatso zimene Mulungu amawatumizira iwo. Chabwino.

<sup>36</sup> Tsopano, anthu oyambirira anadzilekanitsa okha ku kukhulupirira Mulungu, posawakhulupirira Mawu Ake ndi kumvera bodza la mdierekezi. Tsopano, ndicho chinthu choyambirira chimene chinalekanitsa chilumikizano chodabwitsa ichi. Tsopano taonani, Adamu ndi Eva anali pamalo akuti sadzafa konse, pamalo akuti sadzakalamba konse, kuti sadzadwala konse, kuti sadzakhalanso ndi nkhwawa.

<sup>37</sup> Inu mukuti, “Ine ndithudi ndikukhumba ndikanakhala monga choncho.” Ndiloleni ine . . . Ndiri ndi nkhwani kwa inu, inu muli mmalo omwewo. Mulungu amayika izo kwa cholengedwa chirichonse pa dziko lapansi, mmalo omwewo.

<sup>38</sup> Kodi mgwirizanowo unali chiyani? “Ngati musunga Mawu Anga! Ngati, Mawu Anga, ngati inu mungawasunge Iwo, kuwakhulupirira Iwo ndi kuchita pa Iwo!” Koma nthawi yoyamba yomwe Eva sanakhulupirire, anachotsa Mawu amodzi kuchoka ku zomwe Mulungu ananena, izo zinadula chiyanjano ndi chilumikizano chachikulu chimenecho. Ndipo miniti imene mpingo sukhumupirira Mawu amodzi aliwonse a Baibulo la Mulungu, ndi kukawayika Iwo kwinkwakwake, ndiye iwo amadula chiyanjano chodabwitsa chimenecho chimene chaperekedwa kwa iwo, ndi kukhala olekanitsidwa. Mwamsanga pamene iye anachita zimenezo, imfa inadzalowa mwa umunthu wake wachivundi. Osati kokha lachivundi lake, koma umunthu wake wauzimu. Iye anadula ubale wake ndi Mulungu, miniti imene iye sanakhulupirire. Ndipo palibe munthu angakhoze kukhumupirira . . . Ndi izi apa! Palibe mwamuna, palibe mkazi angakhoze—angakhoze kukhumupirira bodza la mdierekezi mpaka iwo atakhala osakhulupirira Choonadi cha Mulungu. Palibe amene angakhoze kukhumupirira bodza la mdierekezi mpaka iwo atakhala osakhulupirira Choonadi cha Mulungu. Chotero, inu mwaona, Eva, Adamu, pamene izo zikutiyika ife mmawa uno?

<sup>39</sup> Tsopano tiyeni tilingalire motsimikiza, chifukwa ife sitidzathanso konse kuganiza zikatha izi, moyo wachivundi uwu ukatha. Kuganiza kwanu kuli tsopano. Inu simudzakhoza kudzasankha zikadzatha izi, mukuyenera kusankha tsopano, pakuti ili ndi tsiku la kusankha, kupanga chisankho chanu. Tsopano iye, Mawu amodzi, osati Malamulo onse, Mawu amodzi basi, iye anamukaikira Mulungu chifukwa izo zinaperekedwa kwa iye mu kuwala kuja, kuti Mawu amenewo anali okayikitsa. Mawu a Mulungu sangakhoze kukaikiridwa, Iye ankatanthauza zomwe Iye ananenazo. Koma iye anawakaikira Iwo chifukwa izo zinaperekedwa kwa iye, “Oh, Mulungu ndithudi sankatanthauza zimenezo.” Koma Iye ankatanthauza zimenezo! Mulungu amatanthauza Mawu aliwonse amene Iye awanena. Ndipo Iwo

samasowa kutanthauzira kwamseri kulikonse, Iwo amakhala momwe Iye anawanenera Iwo.

<sup>40</sup> Chabwino, mukuti, “Mmene mumadziwira za Baibulo.” Ine ndikuhulupirira kuti Mulungu wanga walitsogolera Baibulo ili, Iye amayang’anira pa Mawu Ake. Iye ankadziwa kuti osakhulupirira Mulungu ndi achikunja adzawuka mmasiku otsiriza, chotero Iye waliyang’anira Ilo. Izi ndi ndendende zomwe Mulungu ankatanthauzira Ilo. Ndi momwe Ilo liriri kwa ife tsopano. Tsopano ife tikuyenera kulikhulupirira Ilo. Mawu amodzi kuchoka kwa Ilo, ndipo ife timataya chiyanjano chathu, kupita mu—ku imfa, kulekanitsidwa Kwamuyaya kwa Mulungu, chimodzimidzi monga mome Adamu ndi Eva anachitira. Ife tikuyenera kukhulupirira Choonadi cha Mulungu.

<sup>41</sup> Mundilole ine ndibwereze zimenezo kachiwiri. Musati musamakhulupirire Mawu aliwonse a Baibulo la Mulungu. Koma osati kungonena, “Inde, ine ndimakhulupirira Ilo.” Kuti “koma”? Ayi, palibe kanthu za izo. Inu muzilikhulupirira Ilo, inu muzilivomereza Ilo. Ngati muliyika Ilo pambali, kumati, “Chabwino, mpingo wanga sumakhulupirira Ilo mwanjira imeneyo,” ndiye inu simukukhulupirira kuti Ilo ndi Mawu a Mulungu, ndipo inu mudzapita kutali pansi pa kutsutsika komweko kumene Eva anachoka ali pansi pake. Inu munadzilekanitsa nokha kuchoka ku Wamuyaya pamene inu munali nawo mwayi woti mulumikizane ndi Iye. Tsopano, kumbukirani, Ilo silingatsutsidwe, chifukwa Ilo linali Mawu amodzi, amenewo, mu Mawu a Mulungu.

<sup>42</sup> Ndipo, tsopano, ngati Mulungu akanangokhala ndi a—Mawu ochepa pamenepo omwe anthu akuyenera kuwamvera, ndipo mu Mawu ochepa amenewo amodzi a iwo anaperekedwa molakwika, anayambitsa imfa, tayang’anani pa Mawu amene ife tiri nawo lero! Mukuona? Ife tikuyenera kulandira aliwonse a iwo, tigwiritsitse kwa iwo ndi kulowa mwa iwo monga malonjezano ochokera kwa Mulungu. Ndipo mkazi woota wa Mulungu adzachita zimenezo, wotomeredwa wofunsiridwa woota. Tsopano, ine ndikuyembekeza zinthu zazing’ono izi zipita pansi mwakuya tsopano kuti ife tikhoze kuzigwira izo.

<sup>43</sup> Kodi chinthu choyamba chinali chiyani chimene chinampangitsa Eva kusakhulupirira Mawu a Mulungu? Chinali chifukwa Satana anamulonjeza iye nzeru zochulukira, “Iwe udzakhala wanzeru.” Tsopano, inu mukuona, mtundu wa anthu nthawizonse umafunafuna chinachake. Ndipo Eva ankafunafuna nzeru zochulukirapo.

<sup>44</sup> Tsopano tiyeni tiyime miniti imodzi yokha. Kodi chimenecho sichiri chikhalidwe cha dziko lero? Iwo akufuna nzeru zochulukirapo, kalasi yabwinoko, ophunzira apamwamba, kufuna chinachake chosiyana, nzeru zochulukirapo. Ndicho chimene Eva ankafuna. Koma mundilole ine ndinenenso ichi,

kuti palibe nzeru imene ingapitirire ya Mulungu, komabe Iwo ali mu mawonekedwe odzichepetsa chotero kuti anthu amawaphonya Iwo.

<sup>45</sup> Satana, monga ine ndanenera nthawi zambiri, amanyezimira, koma Uthenga umawala. Oh, pali kusiyana kwakukulu pakati pa kunyezimira ndi kuwala. Hollywood imanyezimira, koma Mpingo umawala ndi mphamvu ndi chikondi cha Mulungu. Hollywood imanyezimira. Pali kusiyana ndithu pakati pa kuwala ndi kunyezimira. Ife sitimafuna kuti tizinyezimira. Ife timafuna kuti tiziwala.

<sup>46</sup> Lero, ndizoyipa kwambiri kuti tiziganiza izi, koma mipingo imayesera kutsamira pa kumvetsa kwawo kwawo, ndendende basi monga Eva anachitira. Iye anaganiza, chifukwa izo zinaperekedwa kwa iye, izo zinkawoneka zenizeni kwambiri. Oh, musalephere kumvetsa izi. Zinkawoneka zenizeni kwambiri, chinachake chimene chikanakhoza kuwonjezeredwa ku chimene Mulungu ananena. Zinkawoneka ngati kuti iye akanakhala ndi chinachake chimene Mulungu anali asanamuuze iye utali wa mmene iye akanapitira. Mulungu anali asanamupatse iye mzere wamalire monga Iye anayikira nyanja ndipo iyo siingadutse chifukwa mwezi umayang'anira iyo. Iye anaganiza...Iye ankaganiza kuti Satana anali ndi chinachake pa mpira, monga ife timanenera, kuti iye akanakhala mu chilumikizano ndi Mulungu, ndipo komabe kukhala wanzeruko, iye akanakhala ndi maphunziro abwinoko. Koma Mulungu anali atamupatsa iye ndendende basi chimene iye ankachisowa.

<sup>47</sup> Ndipo Iye wapereka kwa mpingo chinthu chomwecho. Kumeneko sikupotoza kwa seminar, kapena kubwera kapena kupotoza kuchokera ku a—sukulu ya Baibulo. Koma Iwo ndi ndendende zomwe zinalembedwa, ndipo PAKUTI ATERO AMBUYE! Sitingawasinthe Iwo! Koma mipingo imatsamira pa kumvetsa kwawo. Iwo—iwo amaganiza kuti mwina wake ndi a...pali chinachake chokonzedwa kwa iwo, ndipo icho ndi chonyenga.

<sup>48</sup> Ine ndingoyenera ndidikirire pano miniti. Dziko lonse lapansi likukhazikika pa izo. Chuma chonse cha fuko lino chakhazikika pa lingaliro labodza. Ndikuuzani nthabwala pang'ono ya inemwini, iyo si nthabwala; koma inu mukudziwa tonse a ife timawakonda akazi athu, kapena, ife tikuyenera. Ndipo ine ndinkawonera pa purogramu kuno nthawi ina kale kunja Kumadzulo, yakhala ili nthawi yaitali yapitayo, pafupifupi zaka zitatu. Ndipo mchipinda changa mmawa wina ine ndinadzuka, ndipo munali televizioni mu chipindamo. Ndipo ine ndinaganiza, “Zikuwoneka ngati nyengo yoyipa.” Ndipo ine ndinaganiza, “Chabwino, pa eyiti koloko iwo akuyenera kukhala ndi nkhani.” Ndipo ine ndinatenga kabukhu kakang'ono, iko kanati nkhani pa nthawi inayake.

<sup>49</sup> Ine ndinatsegula nkhanizo, ndipo pamene ine ndinali kumvetsera nkhanizo, kenako ndinazindikira kuti pakati pa nkhanizo anayimitsa kuti asatse mtundu wina wa katundu, mtundu wina wa sopo. Ndipo anati, “Simukusowa kuti muzitsuka mbale zanu panonso, adona. Chinthu chokhacho chimene inu mungachite ndi kuziyika izo mmadzi ndi kuzilola izo zikhale mmenemo kwa maminiti angapo, kuzitulutsamo izo ndi kuziyika pa thandala lowumitsira, izo zonse zatha.”

<sup>50</sup> Ine ndinaganiza, “Ndikakhala ngwazi ndikakafika kunyumba.” Ine ndinalembe dzina lake pansi, chinthu chinachake ichi. Ine ndinati, “Ndikamuuzza mkazi wanga, ‘Ukuwona chimene ine ndingakhoze kuchita!’”

<sup>51</sup> Chotero ine ndinapita ndi kukatenga botolo la chinthu *chakuti-ndi-chakuti*, ndipo ine ndinachithira icho chonse mmadzi. Ndinamuuzza iye kuti apitirize kusesa m’nyumba, ine ndimukonzera iye zimenezo. Chotero ine ndinatenga mbale za ana ndipo ndinachotsa zinyenyiswa, ndi zina zotero, ndi dzira litamatirira pa izo, ndipo ndinaziponyera izo mmadzi ndi kulola izo zikhale maminiti pang’ono, ndi kuzitenga izo ndi kuziyika izo pamenepo. Panali dzira lochuluka basi pa izo monga zinaliri pamene ine ndimayika mmenemo. Mwaona, ine—ine ndikanataya. . . Mkazi wanga akanataya chidaliro mwa ine nthawi imeneyo.

<sup>52</sup> Inu mwaona, nchifukwa chiyani fuko, nchifukwa chiyani izi. . . fuko lino limalola anthu azinyengedwa? Izo sizikuyenera kuloledwa kuti zizinedwa monga choncho. Zimenezo zikuyenera kukhala zotsutsana ndi lamulo. Za kusatsa ndudu yamakono, ndi chamanyazi bwanji, “Osatsokomola mgalimoto yodzaza,” zonse za mtundu umenewo. Izo sizikuyenera ziziloledwa. Kodi izo zikuchita chiyani? Izo zikunyenga. Muli imfa mu chirichonse cha izo. Muli imfa mu kumwa kachasu; kugwiririra, kupha, misala, mu botolo. Koma komabe ife timaloledwa kuziyika izo pa maprogramu athu ndi kuzilengeza izo ngati “Mtundu umene agogo ankamwa. Chisangalalo chochuluka mmoyo,” mitundu ina ya zakumwa za mowa ndi kachasu. Ndi chiyani icho? Ndi kunyenga. Ndi kuyika chinachake pamaso pa anthu kuti adziphe nacho. Ndipo ife timaloledwa kuchita izo.

<sup>53</sup> Ndipo ndiloleni ine nditembenezire izo mmbuyo momwe. Ndipo mipingo kudzera mu chiphunzitsa chopangidwa ndi anthu, tizikhulupiriro topangidwa ndi anthu tikupereka kutsogolo kwakukulu kwa anthu, ndipo iwo akugwera kwa izo, yomwe ili imfa. Palibe mpingo umene udzayeretse solo yanu. Palibe kachikhulupiriro kangakhoze kuyeretsa solo yanu. Magazi a Yesu Khristu okha ndi omwe angathe kuyeretsa solo yanu, mankhwala a Mulungu, Iwo ndi oyikiridwa kumbuyo. Chotero ndi zabodza basi, koma anthu amadalira kumvetsa kwa anzeru, ndipo amafa nazo izo. Ndipo anthu lero akudalira

pa kumvetsa kwa—kwa tizikhulupiriro ndi zipembedzo, ndipo mamillionsi ngati nkhumba zophedwa akuponyedwa m'dzenje lopanda malire la gehena. Ndi zamanyazi bwanji. Ife timaletsedwa kudalira pa kumvetsa kwathukwathu. Ife sitingathe kuyesera.

<sup>54</sup> Inu mukuti, “Kodi gulu la anthu silikuyenera kunena zambiri za Iwo kuposa munthu mmodzi?” Osati ngati munthu mmodzi ameneyo anena Mawu a Mulungu. Panali aneneri foro handiredede nthawi ina anabwera pamaso pa mafumu awiri, ndipo iwo anadalira kumvetsa kwawo komwe. Koma panali mmodzi yemwe anakhala ndi Mawu a Mulungu ndipo izo zinatsimikizira kuti iye anali kulondola, Mikaya. Izo zimatengera ngati iwo ali Mawu a Mulungu. Chirichonse chotsutsana ndi Mawu ndi cholakwika, chimabwera mu imfa. Palibe nzeru imene ingapose nzeru ya Mulungu. Iye ndi wanzeru kuposa anzeru onse. Iye ndi—Iye ndi Kasupe. Iye ndi gwero lokhalo la nzeru. Mawu a munthu aliyense ndi opusa ndi bodza, koma a Mulungu, ngati iwo ali otsemphana ndi a Mulungu. Tsopano, ngati munthuyo akunena Mawu a Mulungu, ndiye izo—si mawu a munthu kose, ndi Mawu a Mulungu. Mwaona, uko sikumvetsa kwa munthu.

<sup>55</sup> Satana adzakupangirani inu malonjezo amtundu uliwonse, koma iye alibe kalikonse koti akupatseni inu, chifukwa iye alibe kanthu. Iye alibe chipulumutso. Kodi Satana ndi chiyani? Chirichonse chotsutsana ndi Mawu. Iye alibe chipulumutso, iye alibe Kuwala. Ufumu wake ndi mdima, mapeto ake ndi imfa. Mdima ndi imfa ndi ufumu wa Satana. “M'bale Branham, tabwerezaninso zimenezo. Kodi ufumu wa Satana ndi chiyani?” Chirichonse chotsutsana ndi Mawu a Mulungu.

<sup>56</sup> Tsopano, izo zikucheka, koma ndi nthawi yocheka. Mukuona? Nthambi, mtengo, ngati iwo uti udzabereke, ukuyenera kusadzulidwa. Ndi nthawi.

<sup>57</sup> Chirichonse chotsutsana ndi malangizo a Mulungu, Mawu a Mulungu, si Mulungu. Ndi chiyani icho, tchimo ndi chiyani? Chirungamo chopotozedwa. Kodi imfa ndi chiyani? Moyo wopotozedwa. Kodi ufumu wa Satana ndi chiyani? Chirichonse chimene chikuyika chinachake kuti chitenge malo a Mawu, chirichonse, chiphunzitsa chirichonse. Mawu amodzi, mawu amodzi okha. Inu mukhoza kukhulupirira chidutswa chirichonse, Eva anakhulupirira chidutswa chirichonse cha Iwo ku Mawu amodzi amenewo. Mawu amodzi amenewo ndi onse amene iye ankasowa kuti asawakhulupirire. Mawu amodzi amenewo ndi onse amene inu mukusowa kuti musawakhulupirire.

<sup>58</sup> Tsopano tiyeni tiyang'ane pa izo. Njira yokhayo yokhalira mu chiyanjano Chauzimu, inali kusunga Mawu amenewo. Mulungu anati, “Inu muzichita *ichi*. Inu musachite *ichi*. Inu muzichita *ichi*, ndipo inu mukhoza kuchita *ichi* ndi kuchita

*ichi*. Koma musadzachite *ichi*.” Tsopano, chidutswa chimodzi chaching’ono chokha cha lamulo chimene iye sanachimvere, ndipo chinayambitsa chinthu chonsecho. Chifukwa iye anachita izo, zinapangitsa mwana aliyense wanjala amene anakhalapo mu dziko, ululu uliwonse wa imfa, chisoni chirichonse, kupweteka kwa mtima kulikonse. Iye anachita izo pomwepo. Ndi chinthu choyipa bwanji, kusakhulupirira Mawu a Mulungu. Munthu aliyense yemwe amabuula mu zowawa za imfa iliyonse yomwe inayamba yakhalapo kapena yomwe iti idzakhalepo, iye anachita izo nthawi yomweyo. Mwana wamng’ono aliyense wosakwatiwa, iye anachita izo nthawi yomweyo, mwana aliyense wobadwa pansi . . . kunja kwa banja. Tchimo lililonse limene linayamba lachitidwapo, iye analiyambitsa ilo apo pomwe posunga Mawu aliwonse mpaka pansi kupatula malo amodzi aang’ono apa. Iye—iye analingalira. Iye basi . . . Iye sananyalanyaze izo. Iye ankadziwa izo, koma iye basi . . . Iye ananyezengedwa kuti achite chinachake chabwinoko chifukwa analonjezedwa gulu labwinoko la anthu, nzeru yabwinoko, kudziwa zambiri za Iwo ngati iye akanachita *ichi*. “Atumiki athu ndi ophunzira bwinoko. Ife tiri ndi gulu labwinoko.”

<sup>59</sup> Palibe gulu labwinoko la anthu padziko lapansi kuposa iwo amene amasunga Mawu a Mulungu. Ndicho chopambana. Ndiro gulu lokhalo limene Mulungu amaliyang’ana. Kanthawi pang’ono chabe ndipo mwinamwake Mulungu adzatilola ife kulowa mu izo.

<sup>60</sup> Ufumu wake sungakhoze kulonjeza chirichonse koma imfa. Ndizo zonse zomwe iye ali nazo. Iye ndi woyambitsa wa imfa. Iye akhoza kulonjeza mabodza chifukwa iye ndi atate wa mabodza. Iye sangakupatseni inu Moyo. Iye sangakupatseni inu Kumwamba, iye alibe Kumwamba kuti akupatseni inu.

<sup>61</sup> Taganizani za zimenezo! Mawu amodzi, kusamukhulupirira Mulungu kudzera mu lonjezo la mdierekezi kapena makina ake, Mawu amodzi, amakutumizani inu ku mazunzo. Umo ndi momwe izo zinayambira. Ndipo ngati Mulungu, mu chifundo Chake momwe Iye aliri, anatumiza unyinjira uyu wa gehena pa dziko lapansi, ndi kupangitsa ana aang’ono anjala, mitundu yonse ya masautso, ndi anthu anjala, ndi imfa mdziko lapansi, chifukwa Mawu amodzi, pachiyambi, kodi Iye sakanakhoza kuziyang’ana izo ndi kubwera kuti pasakhale unyinjira wa mazunzo onsewa? Kodi Iye sakanakhoza kuchita zimenezo? Ndiye ngati Iye sanakhululukire Mawu amodzi kumeneko, akudziwa kuti izi zikanadzakhala zotsatira zake, ndi mochulukira bwanji kuti Iye sangakhulukire Mawu amodzi pamene pamene mmodzi adzakhala wovutika yekha, amene sakhulupirira. Taganizani za zimenezo, ndi chinthu chopambana.

<sup>62</sup> Tsopano, pamene Adamu ndi Eva anamvetsera ku bodza la mdierekezi, chifaniziro choyera cha Mulungu chinawasiya iwo,

chiyanjano chawo chinaweka ndi Mulungu. Chiyanjano chawo cha amodzi ndi Mulungu chinaweka. Miniti yomweyo imene iwo anamvetsera ku bodza la mdierekezi, izo zinaswa chiyanjano chawo. Ndipo miniti yomweyo imene inu mumvetsera ku bodza la mdierekezi, ilo lidzaswa chiyanjano chanu. Ndiyo miniti yomweyo imene inu mudzachoke pa Kukhalapo kwa Mulungu, monga iye anachitira, ndi pamene inu munalephera kutenga Mawu a Mulungu monga momwe Iwo aliri.

<sup>63</sup> Tsopano taonani, ine ndikufuna ndikufunsemi inu chinachake. Ife tonse tikudziwa kuti Mulungu alipo. Ndipo ngati Mulungu ali wolondola kwambiri ndi Mawu Ake, ndipo wotsimikizika kwambiri kuti Iye adzaweruzana anthu ndi Mawu Ake, ndiye Iye akuyenera kukawasunga Mawu penapake kuti adzaweruzire nawo anthu. Baibulo ili ndi Iwo. Inu musayiwale zimenezo. Ndi Baibulo limene Mulungu ati adzaweruze nalo anthu, pakuti Ilo linanena mu Chivumbulutso 22, “Iye amene adzachotsere Mawu amodzi kwa Iwo kapena kuwonjezera mawu amodzi kwa Iwo.”

<sup>64</sup> Onani, osati kungonena, “Chabwino, ine—ine ndimapita ku tchalitchi. Ine ndimakhulupirira. Ine—ine—ine ndimakhulupirira Mulungu.” Bwanji, mdierekezi aliyense mu gehena amamukhulupirira Iye. Aliyense wa iwo ndi wachipembedzo, aliyense.

<sup>65</sup> Koma zimangotengera mawu amodzi, amene amaswa chiyanjano apo pomwe. Unyolo sumakhala wamphamvu kuposa polumikizira pake pofooketsetsa. Ndipo pamene kufooka kwanu kuli pa kusakhulupirira Mawu a Mulungu, pamenepo ndi pamene inu mumafuna kuyikapo cholumikizira chatsopano, cholimba ndi zina zonsezo. Ngati inu mumakhulupirira kuti Yesu Khristu amapulumsa, ndiye inu mukuyenera kuyika cholumikizira mmenemo chimene chimakhulupirira kuti Iye amachiritsa. Ngati inu mumakhulupirira kuti Iye anali, inu mukuyenera kukhulupirira kuti Iye alipo. Aleluya! Ngati inu mumakhulupirira kuti Iye anali, ndipo nkumadabwa ngati Iye ali, cholumikizira chimenecho chidzaduka, ndiye inu mwatayika. Mukuona chimene ine ndikutanthauza? Ndi zokhwima, ndi zovuta, koma ndi Choonadi. Inu mukuyenera kumukhulupirira Iye, Mawu aliwonse, chirichonse chimene Iye ananena.

<sup>66</sup> Tsopano, inu mukuti, “Chabwino, tsopano, M’bale Branham, nanga bwanji zipembedzo izi?” Chabwino, tsopano mveterani. Ngati iwo akhala ndi Mawu awa, chabwino. Koma ngati iwo akuwakana Mawu amenewo, ndiye si zolondola, ndi mdierekezi kachiwiri. Mukuona?

<sup>67</sup> “Nanga bwanji mpingo wakuti-wakuti uwu?” Ine sindikudziwa chiyani za mpingo umenewo. Chinthu chokha chimene ine ndikuchidziwa ndi Mawu awa. Tsopano, inu



mukhulupirira bwanji mpingo pamene kuli zipembedzo naini handirede ndi chakuti zosiyanasiyana, ndipo chirichonse kumati “chipembedzo chathu chiri ndi ndendende Choonadi”?

<sup>68</sup> Tsopano kodi inu mungapite kuti? Inu mukuyenera kukhala ndi chikhulupiriro mu chinachake. Chabwino, inu mukuti, “Ine ndiri ndi chikhulupiriro mwa a Methodisti, mwa a Baptisti, mwa a Presbateria, mwa Achilutera, mwa a Pentekoste, mwa Akatolika,” chirichonse chomwe Icho chiri. Inu muli ndi chikhulupiriro mu bungwe limenero, ndipo, ngati izo ziri zotsutsana ndi Mawu, inu mukuchita chinthu chomwe chomwecho chimene Eva anachita. Ndendende! Inu mukuchita ndendende chinthu chomwecho chimene iye anachita, kutenga Mawu a Mulungu ndi kuwapanga Iwo . . .

<sup>69</sup> “Chabwino, pali gulu labwinoko la anthu limapita kuno. Ndi nyumba yokulirapo. Iwo ndi amuna anzeru.” Zimenezo sizimakhala ndi kanthu kamodzi kochita ndi izo. Satana ndi wanzeru kwambiri kuposa Eva. Iye sanati . . . sanali nkomwe mu chithunzicho. Koma iye sankayenera kukhala wanzeru, iye an kayenera kukhala womvera. Iye sitikuyenera kukhala anzeru. Yesu anati ana a dziko lapansi, kapena, ufumu wa dziko lapansi lino ndi anzeru kwambiri, ana a mundima kuposa ana a Kuwala. Iye timafanizidwa ndi nkhosa. Nkhosa sizingathe nkomwe kudzitsogolera zokha, izo zimayenera kukhala ndi m’busa. Mulungu samafuna kuti tikhale anzeru, Iye amafuna kuti tizidalira pa kumvetsa Kwake, ameni, basi kumene Iye akutitsogolera. Ameni. Inu mukuchiwona chithunzicho? Musadalire pa kumvetsa kwanu kwanu. Miyambo 5, 3. Musadalire pa kumvetsa kwanu kwanu, muzidalira pa kumvetsa Kwake. Ziribe kanthu momwe zikuwonekera mosemphana, ndi momwe nyali zowala zikuwonekera zazikulu kunja kuno, musapereke chidwi kwa izo. Muzingodalira pa kumvetsa Kwake, chimene Iye ananena ndi Choonadi.

<sup>70</sup> Tsopano, umodzi mu chiyanjano unasweka pakati pa Mulungu ndi ana Ake, miniti yomwe iye sanakhulupirire ndime imodzi yaing’ono, Mawu amodzi aang’ono a Mulungu. Aliyense amene wamvetsa izi, nenani, “Ameni.” [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Osati Baibulo; kuti, “Ine sindimakhulupirira Baibulo konse. Ine ndimakhulupirira theka la Ilo.” Iye an kayenera kukhulupirira lonse la Ilo, chidutswa chirichonse.

<sup>71</sup> Osati zokhazo, komanso umodzi pakati pa mwamuna ndi mkazi unasweka. Ine sindimakhulupirira pali ukwati uliwonse umene ungakhalepo momwe ukuyenera kukhalira popanda chilumikizano pakati pa mwamuna ndi mkazi ndi Mulungu. Uko nkulondola. Iwo adzabereka ana m’dziko, ndipo adzawapanga iwo a pathengo, kuwapatsa iwo ndudu, kachasu, kusewera njuga pamaso pawo, kumamwa mowa pamaso pawo. Ziribe kanthu momwe iwo aliri okhulupirika ku malumbiriro awo a chikwati,

izo ndi zadama, izo nzachithupi. Koma muli mzimu mmenemo, mzimu uwo wa abambo ndi amayi ochimwa, ziribe kanthu ndi okhulupirika chotani kwa ana awo, izo zidzabwera molakwika.

<sup>72</sup> Chabwino, inu mukuti, “Ine ndikuwadziwa amuna ndi akazi amene sankawaphunzitsa ana awo zimenezo, ndipo sanali Akhristu.” Chinthu chomwecho chosawatsogolera iwo kwa Khristu chinali chinthu cholakwika kwambiri chimene iwo akanakhoza kuchita pambali pa chinacho; osawatsogolera iwo kwa Khristu, mwaona. Chotero inu simungakhale ndi chilumikizano cholondola popanda icho. Chiyanjanocho chasweka.

<sup>73</sup> Ndiye mwamsanga pamene chiyanjano chinaweka pakati pa Adamu ndi Eva. . . Mwamsanga pamene chiyanjano chawo chinaweka pakati pa Mulungu ndi iwo, ndiye chiyanjano chawo pakati pa wina ndi mzake chinaweka.

<sup>74</sup> Mvetserani! Nthawi iliyonse mpingo ukaswa chiyanjano chake, kuti udziponyere wokha mu bungwe, chiyanjano cha okhulupirira chinasweka. Iye tikuyenera kukhulupirira ndi mtima umodzi, malingaliro amodzi, ndi mgwirizano umodzi. Umo ndi momwe iwo analiri chilumikizanocho chisanapangidwe konse pa Tsiku la Pentekoste; mtima umodzi, malingaliro amodzi, ndi mgwirizano umodzi. Ndipo pamene inu muwuponyera mpingo mu bungwe, inu mudzapeza mitundu yonse ya magawano mmenemo. Chifukwa, ena a ana anawo mmenemo akhulupirira mwa Mulungu, iwo adzagwiritsitsa ku chinthu chimene chiri cholondola, ndipo enawo adzapita njira inayo. Chotero, inu mulibe chiyanjano. Inde.

<sup>75</sup> Chiyani? Kuganiza kwake kunasinthwa. Oh, inde, kuganiza kwake kunasinthwa. Chiyanjano chake ndi mwamuna wake sichinali cholondola. Iwo amayamba kukanirana. Mukuona? Kaganizidwe kake kwenikweni kanasinthidwa. Chifukwa chiyani? Iye anali ndi moyo wa mdierekezi mwa iye. Ndendende! Mwamsanga pamene iye sanakhulupirire Mawu a Mulungu, iye anavomereza moyo wa mdierekezi chifukwa iye anavomereza chiphunzitso chake.

<sup>76</sup> Ine ndikhoza kuzipangitsa izi kukhala zamphamvu moyipa apa, koma izo ziri pa tepi. Ine ndikutsimikiza inu mukumvetsa, Mpingo.

<sup>77</sup> Iye sanawakhulupirire Mawu a Mulungu ndipo izo zinamulekanitsa iye kwa Mulungu, chifukwa mkati mwake pomwepo munali moyo wa mdierekezi. Iye anali atakhulupirira bodza lake, anati, “Zipatsozo ndi zabwino,” ndipo iye anadya izo ndi iye. Uko nkulondola.

<sup>78</sup> Ine sindizigwira Izi, ine ndizilola Izo kuti zibwere mulimonse. Basi sindingakwanitse. Tsiku lina mu California, ine ndikutanthauza mu Arizona, ine ndimaphunzitsa mu tchalitchi. Ine sindinanenepo chirichonse pansa pa kudzodza chimene ine

ndinayamba ndachibwezapo. Ambiri a atumiki ananditsatira ine pa za mbewu ya Satana, mbewu ya serpenti. “Mkaziyo, kunali kudya apulo.” Huh! Izo, chabwino, Kaini ankaganiza chinthu chomwecho, iye anabweretsamo zipatso za mmunda, inu mwaona. Sanali apulo! Kodi iye anazindikira bwanji kuti anali wamaliseche? Ife takhala tikudutsa zimenezo. Izo kwenikweni zinali kugonana. Ndithudi, izo zinali, iye anazindikira kuti anali wamaliseche. Ndipo iye anakhala ndi mwana mwa serpenti, yemwe sanali chokwawa, iye anali wochenjera kwambiri mwa zirombo zonse. Iye anali chinthu chapafupi kwa munthu. Munthu amatha kupeza anyani ndi achiyendayekha—achiyendayekha, ndi zina zotero, koma iwo amalephera kupeza cholumikizira chimene chimamulumikizitsa munthu ndi chirombo pamodzi. Ndi uyo apo. Mulungu anamutemberera iye kutali kwambiri mpaka iye sangathe kubwereranso, izo ziri pa iye chifukwa cha choyipa ichi chimene iye anachita. Iye anali mbewu yokhayo imene ikanakhoza kusakanikirana.

<sup>79</sup> Tsopano, tsiku lina, nditayima, ndikulalikira, panali gulu la anthu Achikatolika mwa omvetsera anga, ndipo ine ndinati, “Inu anthu Achikatolika amene mumamutcha Yesu, kapena, mumamutcha Mariya, kani, ‘amayi a Mulungu,’ Mulungu angakhoze bwanji kukhala ndi amayi pamene Iye ndi Wamuyaya? Iye sangakhale ndi amayi. Yesu sanali nkomwe chirichonse kwa Mariya, koma Iye anali basi... iye anali chofungatira chimene chinamuswa Iye.”

<sup>80</sup> Chabwino, iwo nthawizonse ankakhulupirira, ndipo ine ndinali ndi lingaliro la izo inemwini zaka zapitazo, kuti a—kutenga mimba kwachiyero kunali kwakuti Mulungu anamufungatira iye ndipo anayika khungu la magari mmenemo, koma dzira limachokera kwa mkazi. Ngati dzira limachokera kwa mkazi, pakuyenera kubwera zogirigisha kuti zibweretse dzira kudzera mu chubu kupita ku chiberekero. Mukuona chimene inu mumachita ndi Mulungu? Inu mumamupanga Iye mu nyansi za kugonana. Mulungu, Amene analenga khungu la magari, analenganso dzira, aponso. Dokotala, pakuyenera kukhala mungu wa zonse mwamuna ndi mkazi. Uko nkulondola.

<sup>81</sup> Chabwino, ndiye, ngati mkazi uyu anatulutsa dzira, ndiye Davide akananena bwanji kuti “Ine sindidzamusiya Woyera Wanga Uyo awone chivundi, ngakhalenso Ine sindidzasiya moyo Wake mu gehena”? Ndiye ngati dzira la mkazi linali mwa Khristu, ndiye kuti munthuyo adzakhala ndi chinachake chochita ndi gawo Lake mu chiwukitsiro, pamene izo ndi kwathunthu Mulungu. Nchifukwa chiyani Mulungu anadzutsa chiwalo chogonana cha munthu? Mu chiwukitsiro, nchifukwa chiyani Iye sanasiye thupi Lake kuti liwone chivundi? Chifukwa Iye anali woyera. Ndipo Iye akanakhala bwanji woyera ngati Iye anabalidwa ndi Mariya, ndipo mungu unachokera kwa Mariya, dzira linatsika kudzera mu chubu kulowa mu chiberekero?

Pakanayenera kukhala kugirigisha kwina koti kutsitsire dziralo pansi. Ndiye mkaziyo akanakhala . . .

<sup>82</sup> Chabwino, inu mukuti, “Dziralo likuyenera kuti linali liri pamenepo. Zikanakhala zotheka.” Koma zimenezo, ngati ziri chomwecho, ndiye taonani chimene chikuchitika apa, ndiye kuti Iye sanali palimodzi Mulungu. Iye sanali Mulungu, munga momwe Iye anali munthu. Koma ndiye ngati izo ziri chomwecho, mkaziyo anali ndi chinachake mmenemo. Ndipo a—mbewu yeniyeni imene inachokera kwa Mariya, imene inachokera kwa amayi ake, ndi amayi ake, ndi amayi ake, inali chinachake cha umunthu chosakanizidwa mmenemo, ndi chikhumbo cha umunthu. Sizikanakhoza kukhala. Ayi, bwana. Ine ndinati, “Iye . . . iye anali basi . . .”

<sup>83</sup> Chimodzimodzi munga momwe inu mumaitengera mphungu ndi kuyilola iyo iyikire dzira, ndi kuliyika ilo pansi pa nkukhu, nkukhu yoyi idzaswa dziralo, iye ndi chofungatira chabe. Koma palibe chidutswa chimodzi cha iyo, mphunguyo, chimene chiri nkukhu. Ayi, bwana. Nkukhu yoyi inali . . . Inu mutha kumangirira mwana wagalu pamwamba pa a—dzira la mbalame, ndipo iye angaswe mbalame, mwana wa galuyo angatero. Ndi kutentha kwa thupi komwe kunaswa dziralo.

<sup>84</sup> Ndipo ndi momwe ziliri ndi Yesu. Mariya anali chabe chofungatira. Mulungu anamugwiritsa ntchito iye munga Iye amachitira ndi mkazi wina aliyense. Iye anali namwali, iye analibe ana. Iye anabwera mu chiberekero cha namwali, koma Mulungu Mlengi anapanga ziwiri zonse dzira ndi nyongolotsi, anazilenga izo. Chotero, kunali kutenga mimba kwachiyero.

<sup>85</sup> Pamene ine ndinatuluka, ndithudi, inu mukudziwa abale akundidikirira ine. Iwo anati, “M’bale Branham, ine ndikufuna kuti ndikufunseni inu chinachake. Inu munalakwitsa. Tsopano ife takugwirani inu.”

Ine ndinati, “Chabwino, ndi zomwe ine ndimafuna, kuti ndigwidwe.”

<sup>86</sup> Ndipo anati, “Inu munalakwitsa ponena izi, pamene inu munalalikira *Mbewu ya Serpenti*. Tsopano inu mumanena kuti—kuti dziralo linali la . . . Mulungu analilenga ilo, dziralo. Chomwe chinachitika, ife tikupeza apa kuti mu Genesis mutu wa 3, Mulungu anati kwa Mariya, ‘Ndidzayika udani pakati pa mbewu yako ndi mbewu ya serpenti.’”

<sup>87</sup> Ine ndinaganiza, “Oh, mai!” Ine sindinalalikirepo chirichonse mmoyo wanga pansi pa kudzodza chimene ndinadzachibweza, chifukwa ine sindimadalira pa kumvetsa kwanga komwe. Ndipo ngati kumvetsa kwanga kukhala kotsutsana ndi Mawu a Mulungu, ndiye kuti kumvetsa kwanga ndi kolakwika. Iwo akuyenera kukhala Mawu a Mulungu. Ngati izo si choncho, zisiyeni izo zokha, izo sizoon. Koma tsopano kuwang’amba Iwo ndicho chinthu choyenera kuchita. Mu mtima

mwanga, ine ndinati, “Atate Akumwamba, Inu mundithandize ine. Ine sindikudziwa choti ndichite pano. Munthuyo ali ndi Lemba, iye akulozapo chala chake, ‘Ine ndidzayika udani pakati pa mbewu yako ndi mbewu ya serpenti.’”

<sup>88</sup> Tsopano, ndi izi apa! Mzimu Woyera unasunthira pamenepo. Ine ndimakhulupirira Mmodzi yemwe uja amene anakhoza kumufungatira Mariya, yemwe ndi wokhoza kulenga, Iye akhozanso kuyika Mawu mkamwa mwanu. Ine ndimadalira pa Iye tsiku lililonse. Ndipo nthawizonse amakhala Mawu Ake. Iye sanganene...chinachake chotsutsana ndi Mawu Ake. Ndiye ngati inu mukunena kuti ndinu odzodzedwa, ndipo nkumalalikirira motsutsana ndi Choonadi cha Mulungu, ndiye si kudzoda kwa Mzimu Woyera. Chifukwa, pamene Mzimu Woyera ukufungatirani inu, Iye amabweretsa chinthu chofanana, chifukwa Iwo ndi Mawu.

<sup>89</sup> Mvetserani. Chinachitika ndi chiyani? Ine ndinati, “Chabwino, ine ndikufuna ndikufunsemi inu chinachake. Mkazi alibe dzira. Iye alibe mbewu. Iye anati tsopano, Iye sananene ‘dzira,’ Iye anati ‘mbewu yako.’ Ndipo iye analibe mbewu.”

<sup>90</sup> Zimatengera kulumikizana kuti upange mbewu. Nkulondola uko, adokotala? Zikuyenera kutero. Ngati mutakhala ndi kamtima kunjira kuno, munalibe moyo mmenemo, ndipo nkubzala iko kunjira kuno, iko—iko sikangamere nkomwe, kadzakhala pamenepo nkuvunda. Ndipo inu simungabzale moyo popanda kukhala ndi kamtimako. Chotero, inu mwaona, chinthu chonsecho ndi chilumikizano. Ine ndikuyesetsa kuti ndikuwuzeni inu tsopano za Khristu ndi Mpingo. Ndi chilumikizano. Mwaona, ngati mkaziyo akhala ndi mbewu ya iyemwini ndiye iye sangamasowe mwamuna, iye akhoza kukhala ndi mwana wake iyemwini. Koma iye sangakhale, sangakhale ndi mwana mpaka atakhala ndi mwamuna, chifukwa izo zimatengera awiriwo pamodzi kuti apange mbewu. Nkulondola uko? Mubzale mbewu yopanda moyo mwa iyo, muwone chimene chiti chidzachitike.

<sup>91</sup> Monga iwo ali ndi maneno awa a mkazi uyu akubereka agalu awa kuno. Mwaona, iwo sangakhale moyo. Izo sizingatheke, chifukwa, mwaona, munguwo sungasakanizikane.

<sup>92</sup> Tsopano, zindikirani izi tsopano, a—mkazi sanali mbewu. Chotero, Iye anati, “Ine ndidzayika udani pakati pa mbewu yako ndi mbewu ya serpenti.” Kumuuza iye kuti Iye anali kupita, Iyemwini, kuti akamupatse iye mbewu, osati kudzera mu kugonana, dama. Iye anali woti alenga mwa iye mbewu. Chabwino, inu mukuti, “Kodi imeneyo ingakhale mbewu Yake?” Inde. Iyo ikanadzakhala ya Mariya ndiye Iye atatha kuipereka iyo kwa iye. Ili ndi diso langa, Iye anandipatsa ine ili. Ndi diso langa, koma Iye analipereka ilo kwa ine. Ili ndi dzanja langa,

Iye anandipatsa ilo. Ili ndi liwu langa, koma Iye anapereka ilo kwa ine. Mukuona? Ndipo mbewu imene inali, Mariya . . . inalibe chochita ndi Mariya. Chinali chinachake chimene Mulungu anachita Mwiniwake.

<sup>93</sup> Chotero mbewu imene inali mwa iye pamenepo, inali chilumikizano cha mchitidwe wosavomerezeka, imene inali imfa. Iye anali atapatsidwa kale pakati ndi mbewu ya serpenti, chifukwa iye anali atakhala ndi. . . Ndipo iye anapotoloka ndipo anati, iyemwini, “Serpentiyo anandinyenga ine.” Uko nkulondola. Ndipo, mwamsanga, Kaini anatulukira.

<sup>94</sup> Oh, ife tikudziwa iye anati iye analandira mwana kuchokera kwa Mulungu. Ndithudi, mwana aliyense amene amabadwa, wapathengo ndi china chirichonse, amayenera kubwera mwa kuchita kwa Mulungu. Iye ndi Mmodzi yekhayo Amene angakhoze kupanga moyo. Ndithudi. Uko ndi kulondola.

<sup>95</sup> Mwaona, iye anali kale woti akhale mayi. Ndipo izo nkomwe . . . kokha chimene icho chinachita, chinali kumveketsa chinthu cha mbewu ya serpenti. “Mbewu imene ili mwa inu tsopano yabweramo mwa kulingalira, momwe mwachitira nawo Mawu Anga mosavomerezedwa, ndi chinthu ichi apa, ndipo inu tsopano muli ndi mbewu ya serpenti. Koma ndikupatsani inu mbewu mwa kukhala pakati mwachiyero, ndipo Mbewu Yake idzavulaza mutu wa serpenti, ndipo mutu wake udzavulaza chidendene.” Amen. Mungomulola Mulungu akhale nazo, ngati iwo ali Mawu Ake Iye adzawafikitsa Iwo pochitika.

<sup>96</sup> Ndi chifukwa chake inu mukuyenera kukhala mu chilumikizano ndi Mulungu. Ndi chifukwa chake Petro ananena pa Tsiku la Pentekoste, Yesu atanena “mukawabatize iwo mu Dzina la Atate, Mwana, Mzimu Woyera,” Petro anatembenuka ndipo anati “muwabatize iwo mu Dzina la Yesu Khristu,” chifukwa Dzina la Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera ndi Ambuye Yesu Khristu. Mukuona zimenezo? Zimatengera chilumikizano.

<sup>97</sup> Paulo anali asanamuwonapo Petro, koma Mzimu Woyera womwewo, mu chilumikizano chomwecho (ulemelero!), unamupangitsa iye kunena chinthu chomwecho. “Kodi inu munalandira Mzimu Woyera chikhulupirireni?”

Iye anati, “Sitikudziwa ngati ulipo.”

Anati, “Inu munabatizidwa chotani?”

Anati, “Kwa Yohane.”

<sup>98</sup> Anati, “Inu mukuyenera kuti mubatizidwenso kachiwiri, mu Dzina la Yesu Khristu.” Ndipo iwo analandira Mzimu Woyera.

<sup>99</sup> Chinali chiyani icho? Chilumikizano, kunena chinthu chomwecho chimene Mulungu akunena! Ndipo uko ndiko kuvomereza. *Kuvomereza* kumatanthauza “kunena chinthu chomwecho.” Ndipo Iye ndi Wansembe Wamkulu wa kuvomereza

kwathu, kuchita pa zomwe Iye wanena. Ife timanena kuti Iwo ndi Choonadi, ndipo Iye amachita pa Iwo. Oh, mai! Ndi zimenezotu. Apo pali kutenga pakati.

<sup>100</sup> Tsopano penyani momwe iye—iye—chilumikizano chake pakati pa iye ndi mwamuna wake chinasweka. Mwaona, mofulumira, mwamsanga pamene Mulungu anati “Adamu, iwe wachita bwanji izi?” Mmallo momuyankhira mkazi wake, iye anazikankhira izo kwa mkazi wake. “Mkazi amene Inu munandipatsa ine.” Chilumikizano chinasweka. Mukuona?

<sup>101</sup> Kodi iye anachita chiyani? M'malo moti amukonde mwamuna wake ndi kunena Choonadi, iye ananama. Iye—iye—iye—iye akanayenera kunena kuti, “Iye ndi wosalakwa, ine ndinapereka kwa iye.” Ameni. Baibulo linati, “Iye anapereka kwa mwamuna wake.” Iye akananena kuti, “Mwamunayo ndi wosalakwa. Ine ndinamupatsa iye ndipo iye anadya, koma ine ndi amene ndinapereka icho kwa iye.” Mmallo mwa zimenezo, iye anazikankhira izo kwa serpenti, wolambalala wapafupi kwambiri.

<sup>102</sup> Ndicho chinthu chomwecho chimene iwo akuyesera kuchita lero. Mwaona, mwamuna, mkazi, chilumikizano chinasweka. Mwamuna ndi mkazi, chiyanjano chinasweka pakati pawo. Umodzi wa iwo unasweka, umodzi pakati pa iwo ndi Mulungu unasweka. Chinthu chonsecho chinawonongeka. Chifukwa chiyani? Chifukwa Mawu amodzi sanakhulupiriridwe. Oh, m'bale, mai! Eya, iye ankayenera kunena Choonadi. Umodzi ndi iye ndi mwamuna wake unali utapita, ndipo umodzi wa iwo ndi Mulungu unali utapita. Ndipo mpingo uliwonse umene sumatenga Mawu onse a Mulungu, chinthu chomwecho chimachitika. Ndikuzikonda Zimenezo, sichoncho inu?

<sup>103</sup> Muwoneni mwana wake woyamba kubadwa, Kaini, wakupha, bodza, wachinyengo, wansanje, wansanje ndi m'bale wake. M'bale wake ankasunga Malamulo a Mulungu, ndipo Mulungu anali atapanga chitetezero pakupha nsembe ndi kuyipereka iyo kwa iwo. Penyani umbuli wa izo tsopano, wa Satana, anayesera kulowetsa mmalo chinachake. Mulungu, Baibulo linati, anapita ndipo anakawapangira iwo zovala za zikopa; kuti apeze zikopa, chinachake chinafa. Adamu anayesera kudzipangira yekha zovala kuchokera ku masamba a mkuyu. Izo sizikanagwira ntchito, moyo wa zomera. Moyo, moyo woyenda un kayenera kufa. Chotero Iye anapha moyo wa mawonekedwe wotsika, ndipo akunena mmenemo kuti “Tsiku lina Moyo Wanga Womwe udzaperekedwa kwa inu, Moyo weniweni umene udzakokerenso mu chilumikizano ichi kachiwiri.” Tsopano, ife tifika kwa izo mu maminiti pang'ono, Mulungu akalola. “Mwaona, apa pali moyo wa mwanawankhosa. Tsopano, inu muzivala ichi mozungulira inu ndi kubisa umaliseche wanu.” “Inu musamadye maapulo”?

Zamkutu! Mukuona? “Muyike zikopa izi mokuzungulirani inu.” Iye ankayenera kupha chinachake.

<sup>104</sup> Ndipo mwana wa Satana, sanabwera momwe Iye ankafunira, iye anatero. Mulimonse inu mukufuna kunena izo, koma anali mwana wa Satana, chifukwa chiyero chija cha Adamu kwa Mulungu sichikanabweretsa mtundu umenewo wa chinthu. Zindikirani ndiye mwana wa Satana, akuyesera kuti apange chitetezero, anabwerera ndi chinthu chomwecho chimene anthu ambiri amanena lero, mulu wa maapulo ndi zipatso za mdziko, kuti apereke ngati chitetezero, mankhwala.

<sup>105</sup> Ndipo Abele wolungamayo anachita chiyani? Iye ankadziwa kuti icho sichinali chinthu monga kudya maapulo. Iye anali magazi a amayi ake ndi adadi, moyo wa iwo. Chotero iye anabweretsa mwanawankhosa, monga momwe Mulungu anachitira. Aleluya! Iye anasunga Mawu a Mulungu, ndipo Kaini anamuchitira iye nsanje.

<sup>106</sup> Chinthu chomwecho lero! Chimabwera mu nsembe ya magazi imeneyo, Mawu a Mulungu amenewo ndendende basi zomwe Iwo amanena, muzikhala kumene ndi Iwo. Ambiri a iwo angakhoze kukhulupirira nsembe ya magazi imeneyo, ndithudi, koma ukanena chinachake mu Mawu, iwo amati, “Oh, ayi, ine sindimakhulupirira zimenezo. Uh-huh, izo—izo ndi za tsiku lina.” Mdierekezi wakale yemwe uja, njomba yakale yomweyo! Mudikire mpaka ife tithane nazo izo. Zindikirani, iye akubwera chotsika mwanjira yomweyo.

<sup>107</sup> Koma Kaini, mu njira zake zopusa, osati zopusa kwambiri, koma mu njira zake zothyathyalika, ananyengedwa, ndipo anabweretsamo chipatso. Adamu anasunga. . . Abele anasunga Mawu a Mulungu, iye anabweretsamo mwanawankhosa. Mulungu anati, “Uko nkulondola, Adamu, iwe wasunga. . . Kapena, Abele, iwe wasunga Mawu Anga.” “Kaini, iwe ukudziwa kuti sizinali. . . Kodi Ine ndinawatenga kuti masamba a mkuyu monga momwe abambo ako ankayesera kuchitira? Iwe uli ndi mulu wa mkuyu kapena mphesa kapena maapulo kapena chirichonse chimene iwe uli nacho pano. Ndipo tsopano abambo ako anatenga masamba kuchokera mu mtengo, kuti ayesere kupanga chitetezero, ndipo apa iwe ukuyesera kubweretsa chipatso kuchokera mu mtengo.” Izo sizinali zimenezo! Anali magazi kuchokera ku moyo.

<sup>108</sup> Oh, Mulungu anabweretsa iwo pamenepo, anati, “Ndi awa apa.” Ndipo Abele anapereka yoyenerayo. Kenako m’bale wake anamuchitira iye nsanje. Tawonani chimene iye anachita, iye anamupha m’bale wake. Mulungu anawukitsa wina; monga imfa, kuyikidwa mmanda, ndi chiwukitsiro cha Khristu. Penyani. Mulungu ndiye, Wake. . . Kodi Iye anamuza chiyani Adamu ndi Eva? “Pitirirani ndipo muchulukane ndipo mudzazitse dziko lapansi.” Kumwaza mtundu wa anthu padziko



lonse lapansi, kuchitira kuti Iye azikakhoza kuchita nawo iwo pawokhapawokha mpaka Iye adzakhoze kuwabwezeretsa iwo pamodzi. Kuchita ndi anthu, munthu payekhapayekha, munthu aliyense. Koma iwo sanazifune izo mwanjira imeneyo.

<sup>109</sup> Musaphonye vumbulutso ili. Mulungu, mulole izo zichitike. Mutawona izo momwe ine ndikuziwonera izo.

<sup>110</sup> Mwaona, izo sizinali zimenezo, Mulungu samachita ndi munthu mu gulu. Mulungu samachita nanu inu mu bungwe. Iye amachita ndi inu ngati munthu payekhapayekha, munthu payekhapayekha. Patokha timabatizidwa ndi Mzimu Woyera. Palimodzi timabatizidwa kulowa mu Thupilo pamene tikubatizidwa ndi Mzimu Woyera. Payekhapayekha, mmodzi aliyense kubatizidwa ndi Mzimu Woyera, Mulungu akuchita ndi aliyense. Chimenecho chinali cholinga Chake, kuwamwaza iwo pa dziko lapansi kuchitira kuti Iye adzakhoze kuchita nawo aliyense payekhapayekha.

<sup>111</sup> Koma m'malo mwa zimenezo, chinachitika ndi chiyani? Mulungu anayenera kuwalekanitsa anthu a Kaini kuchokera kwa anthu a Seti. Iye anamuthamangitsa Kaini. Iye anawalekanitsa iwo kuti Iye akhoze kuchita ndi mpingo Wake. Penyani. Kaini analekanitsidwa. Tsopano penyani. Mulungu anamulekanitsa Kaini woyipa wa Eva kwa Seti woyera wa Adamu. Oh! Kodi Iye anachita zimenezo? Kudzera mu mchitidwe wosavomerezeka, mkazi uyu kukhala ndi munthu wina ndipo nkubereka mwana. Mulungu anamulekanitsa mwana ameneyo ndi timibadwo take kwa munthu wolungama ndi woyera uyu, ana ake.

<sup>112</sup> Ndi chinthu chomwecho lero, kulekanitsa, kulekanitsidwa, anawapeza iwo, iwo sanali mu umodzi. Iwo sakanakhoza kukhala ndi umodzi. Kodi usiku ungakhale ndi umodzi ndi usana? Kodi wokhulupirira angakhale ndi umodzi ndi wosakhulupirira? Kodi munthu amene amakhulupirira mu Mawu onse a Mulungu angakhale ndi umodzi ndi iwo amene amangokhulupirira gawo la Mawu a Mulungu? Mulungu amafuna olekanitsa.

<sup>113</sup> Tsopano, Kaini anali mwana wa Eva, iye anati, "Ine ndalandira mwana." Koma Seti anali mwana wa Adamu. Ndipo Mulungu anawalekanitsa iwo chifukwa iye sakanakhoza kulola... Bwanji, iwo akanadzawonongana wina ndi mzake, ana oyipa a Kaini akanadzawononga ana abwino a Seti. Uko nkulondola.

<sup>114</sup> Tsopano penyani! Ndipo ndi mdierekezi wakale yemweyo yemwe anamupangitsa Eva kuti asakhulupirire Mawu amodzi a Mulungu, ndipo anawauza iwo kuti adzipatule okha kwa wina ndi mzake ndi kukhala osiyana, wina ndi mzake, mdierekezi yemweyo anabwera pakati pawo ndipo anadzawabweretsa iwo pamodzi kachiwiri. Kodi inu munamva zimenezo? Nenani,

“Ameni,” ngati inu munatero. [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Iye anawabweretsa iwo pamodzi kachiwiri pansi pa chilumikizano chabodza, kachitidwe ka Mulungu. . . motsutsana ndi dongosolo la Mulungu. Chinachitika ndi chiyani? Kodi iye anachita motani izo? “Ana a Mulungu,” linatero Baibulo, Genesis, “anawona ana aakazi a anthu.” Ana aamuna a Mulungu, ana a Seti, anawona ana aakazi a anthu, ana a Kaini, momwe iwo analiri okongola. Hum! Ndipo, kodi iwo anachita chiyani, iwo anagwa chifukwa cha iwo! Ndipo iwo anadzilumikiza okha pamodzi kachiwiri, chifukwa cha kukongola, kuti “iwo anali okongola powayang’ana.”

<sup>115</sup> Chinthu chomwecho lero! Ndi inu apa, abale. Inu ofooka Achipentekoste, amene Mulungu anakulekanitsani inu ndi kukutumizani inu kuti mukakhale zipembedzo zosiyanasiyana! Inu simungakhoze kuchipanga bungwe chipentekoste. Anakutumizani inu uko kuti mukakhale anthu Ake. Koma inu munawona mipingo yaikulu yabwino ndi zafioloje, inu mwadzipezera nokha masukulu aakulu ambiri ndi zinthu. Ndipo kodi inu munachita chiyani? Inu mwawalumikizanso anthu a Mulungu ndi bungwe, chimene, maziko ake omwe ndi Chikatolika. Zokongola, matchalitchi akuluakulu, anthu ovala bwino, ameya a mzinda ndi ena onse a iwo amabwera, ovala bwino, ophunzira bwino, azaumulungu apamwamba, amadziwa momwe angabwerere pamalo pomwe aliyense amavala zovala zapamwamba kwambiri, ndipo m’busa amangoyima mwangwiro kwambiri pamalo ake. Ndi chiyani icho? Inu mukuyang’ana pa zinthu zimene Mulungu anazitsutsa. Ndipo inu mwawutenga mpingo wa Chipentekoste (Mulungu, mulole izo zikafike pa matepi!) ndipo mwawulumikizitsa iwo mu bungwe. Mulungu sanafune konse kuti Iwo udzalumikizane, Iye ankafuna kuti Iwo udzalekanitsidwe; sanalumikizane konse ndi dziko.

<sup>116</sup> Mdierekezi wakale yemweyo amene anamupangitsa Eva kuti asakhulupirire Mawu a Mulungu ndipo anamuchitira iye choyipa, anabwereranso ndipo anadzawatenga ana a Seti ndi kuwalola iwo kuti awone akazi okongola awa a Kaini, ndipo iwo analumikizana kachiwiri. Ndipo iwo sanali osakhulupirira. Iwo sanali achikominisi. Ayi, ayi. Iwo anali okhulupirira. Iwo anati, “Tsopano mwina Ambuye akhoza kuchita chinachake.” Kapena, oh, ichi monga choncho. Iwo—iwo anali. . . Iwo ankaganiza kuti ankachita chimene chinali choyenera. Ndipo kodi Mulungu ankayenera kuchita chiyani? Kuchotsapo chinthu chonsecho, ankayenera kuchotsapo chinthu chonsecho. Pansi pa chilumikizano chabodza! Iye ankayenera kutumiza chigumula ndi kuwononga gulu lonse. Chiweruzo chinabwera chifukwa cha chilumikizano chabodza chimenecho. Chiweruzo chinakantha Edeni chifukwa cha mgwirizano wabodza.

Tsopano, kodi serpenti anali ndi mbewu? Manyazi pa inu.

117 Chijanjano chabodza chinabweretsa chiweruzo pa dziko lapansi, kwa Eva ndi Adamu, mu Edeni. Ndipo chilumikizano chabodza chinabweretsa chigumula cha chiweruzo cha Mulungu padziko lapansi chifukwa chakuti ana aakazi a Kaini anakopana ndi ana aamuna a Mulungu, ndipo iwo anagwera izo ndipo analumikizana pamodzi kachiwiri. Ndi zimenezotu. Chilumikizano chabodza, “Palibe chimene chikanachitika.” Kodi Mulungu anachita chiyani? Iye anadzawononga chinthu chonsecho, onse kupatulapo Nowa wokalamba wofunika ndi banja lake. Iye . . . iwo anasonkhana pamodzi.

118 Ndipo kachiwiri zitatha izo, itachitika imfa ya Nowa, ndi banja lauzimu la Nowa lija, chinthu choyamba inu mukudziwa, ana a anthu anayamba kuyang’ana kwa wina ndi mzake kachiwiri. Kodi iwo anachita chiyani? Iwo anati, “Tsopano, ife si achikunja, ife tonse timakhulupirira mwa Mulungu.” Chotero iwo anatenga munthu, ngati mtsogoleri, arkbishopu wina wamkulu dzina lake Nimrodi, ndipo iwo anamanga nsanja. Iwo sanali anachikunja. Iwo ankakhulupirira kuti kunalipo Kumwamba. Iwo ankakhulupirira kuti inalipo gehena. Iwo ankakhulupirira mu ziweruzo. Koma ana a Mulungu ndi ana aakazi a anthu, kachiwiri, ndipo iwo anadzipangira okha chilumikizano, mwabodza, ndipo anamanga tchalitchi chachikulu kwambiri, bungwe lalikulu kwambiri, ndipo malo ena onse anali ku—ku Babelo, ankayenera kumakapereka ulemu kwa iwo.

119 Ndipo iwo anati, “Ine ndikuuzani inu zomwe ife tingachite. Inu mukudziwa ife ndi anzeru.” Kodi nzeru zimenezo anazitenga kuti? Kwa mdierekezi. Ndizo ndendende. Iwo anazipeza izo kuchokera kwa mdierekezi monga—monga Eva anachitira. Anazipeza izo kuchokera kwa mdierekezi. Chotero iwo anati, “Tidzipangira tokha bungwe, timukondweretsa Mulungu. Ndipo ndikuuzani inu zomwe ife titi tichite, tidzakhala ndi masitepe aang’ono. Tidzithamangapo ndi kumayimba ndi kumasangalala ndi angelo, ndi kubwerera kumusi kuno ndi kumadzakhala momwe ife tikufunira.” Mdierekezi ameneyo akadali moyo. Mukuona? Izo zinali zotsutsana ndi malamulo a Mulungu. Iwo sanasunge malamulo Ake. Kodi Mulungu anachita chiyani? Chabwino, iwo anamanga nsanja ya Babelo, yabodza kachiwiri, chotero Mulungu anawasokoneza iwo ndi kuwalekanitsa iwo.

120 Mulungu analekanitsanso ndipo anamutumiza Abrahamu wabwino wokalamba wolungama, anati, “Ine ndingokutenga iwe ndi kupanga fuko kuchokera mwa iwe.” Mulungu anawalekanitsa iwo. “Tuluka pakati pawo, Abrahamu, usiye chirichonse mmbuyo.” Ndipo Mulungu sanamudalitse konse iye mpaka iwo atasiya chirichonse kumbuyo, Loti anali wotsiriza. “Tuluka, Abrahamu, udzilekanitse wekha kwa osakhulupirira amenewo. Ndipo ndidzakutenga iwe ndi kupanga fuko kuchokera mwa iwe. Ine ndidzapanga anthu

amene adzasunge malamulo Anga. Ine ndidzawapatsa mwayi wina.”

<sup>121</sup> Abrahamu wokalamba wabwino anapita kukakhala mu dziko lachilendo. Ndicho chimene Abrahamu aliyense amachita, kukakhala mu dziko lachilendo. Chiyani? Kukakhulupirira lonjezo limene linali losatheka, kuyankhula mwaumunthu. Kodi inu mukuganiza kuti madokotala amakono a Kaini amenewo akananena chiyani tsiku limenero? “Psyii, mai, bambo wokalamba, usinkhu wa zaka handirede, adzakhala ndi mwana mwa mkazi, nainte? Oh, ndi chinthu chopusa bwanji!” Koma Abrahamu ankakhulupirira Mawu a Mulungu. Ndipo chirichonse chotsutsana ndi chimenecho, iye anachitcha ngati kuti icho panalibepo.

<sup>122</sup> Maubatizo abodza onse awa, zogirigisha zabodza, zinthu zabodza zomwe zikuchitika lero, kumati palibepo pamenepo, khulupirirani Mawu a Mulungu ndipo zipitirirani kumapita. Ndi chopunthwitsa chabe kuti musafikire ku chenichenicho. Uko nkulondola. Zisunthiranibe patsogolo, ana. Mawu a Mulungu, Mulungu amasunga Mawu Ake. Ine sindikusamala kuti ndi zinthu zingati zabodza zomwe mdierekezi amaponyera kunja uko, Mulungu akadali ndi Mawu owona ndipo Iye amawasunga Iwo.

<sup>123</sup> Abrahamu anatcha chirichonse chotsutsana, cholakwika. Aroma, mutu wa 4, ngati inu mukulemba zimenezo. Abrahamu anatcha chirichonse chotsutsana ndi Mawu a Mulungu, ngati kuti panalibepo. Uko nkulondola. Iye ankakhulupirira mwa Mulungu, anali wamphamvu, zinalibe kanthu momwe thupi lake linkakhalira lofooka, momwe izo zinkawonekera kukhala zosatheka kuti izo sizidzachitika, Abrahamu anapitirirabe kumakhulupirira izo. Tsopano, iye sankasowa kuti apite akagwade pa guwa ndi kukati, “Ngati sizibwera pakali pano, ine ndichita... Ine sindikudziwa kaya ndikhulupirire kapena ayi.” Abrahamu anakhala ndi izo kwa zaka twente-faivi izo zisanafike, koma izo zinafika kumeneko. Izo nthawizonse zimatero.

<sup>124</sup> Abrahamu, anabwera Isaki; Isaki, anabwera Yakobo; kuchokera mwa Yakobo munadzatuluka mbadwa; kuchokera mwa mbadwa, zinapita ku Igupto; mu Igupto, fuko linakula. Ndiye pamene Iye anakulitsa fuko Lake, zopindula Zake, kodi Iye anachita chiyani? Mulungu anawalekanitsa iwo kachiwiri. Kusakhulupirira ndi chikhulupiriro sizingayendere limodzi. Ayi, bwana. Iye anawalekanitsa iwo kachiwiri, kwa Ake Omwe. Kodi Iye anachita chiyani kwa iwo kuti atsimikize kuti iwo anatsogoleredwa moyenera? Mvetserani mwacheru tsopano, ife tiribe nthawi yochulukwa kwambiri tsopano, mwinamwake maminiti ena fifitini. Iye anawatsogolera iwo pafupi. Penyani, Iye anadzutsa fuko, anawayika iwo pansu pa aphunzitsi ndi zinthu. Iwo anamenyedwa ndi kumalira, ndi kumalira ndi

kumapitirirabe. Koma Mulungu anali akuyang'ana pansi, Iye amakumbukira lonjezo lirilonse limene Iye anamupatsa Abrahamu. Tsiku lina Iye—Iye anaganiza. . . Kodi Iye anachita chiyani kwa iwo? Kodi Iye anachita chiyani pamene Iye anawalekanitsa iwo? Iye anawapatsa iwo lamulo ndipo Iye anawapatsa iwo mneneri, Iye anawapatsa iwo Lawi la Moto. Kodi Iye anachita chiyani? (O Mulungu!) Iye anawuyika mpingo Wake mu dongosolo. Lawi la Moto, Mzimu, kuti ziziwatsogolera iwo, mneneri yemwe akanadzamawawuza iwo Choonadi cha Mawu Ake. Iwo anali okonzekera ulendowo pamenepo. Kodi izo sizodabwitsa?

<sup>125</sup> Kunja mu chipululu iwo anapita, akuchita zizindikiro ndi zodabwitsa, kutsegula Nyanja Yofiira, kuyitanira miliri ya gehena pa Farao. Oh, mai! Lawi la Moto likuyenda patsogolo pawo, ameni, linkawatsogolera iwo usiku ndi usana. Aleluya! Mneneri, woona ku Mawu amenewo, atayima pamenepo akuwasunga iwo mumzere. Ameni. Iye anali wokonzeka kuti awatenge ana Ake pamenepo. Imeneyo inali nthawi yoyamba imene iwo anayamba atchedwapo mpingo. Icho chinali choyimira cha chimene Iye ati adzachite mmasiku otsiriza. Tifikanso ku izo mu miniti yokha. Iye anawayitanira iwo kunja, anawapatsa iwo lamulo, anawapatsa iwo Mawu Ake, ndipo anawapatsa iwo mneneri, Iye anawapatsa iwo chizindikiro, ndipo Iye anawatumiza iwo mu chipululu. Anawalekanitsa iwo ku dziko lonse.

<sup>126</sup> Kodi iwo anachita chiyani? Anawona akazi okongola aku Moabu, mpingo wofunda wokhala ndi milungu ndi milungu yaikazi ndi china chirichonse. Kodi iwo anachita chiyani? Anawatsatira iwo, anakwatira pakati pawo. Ndiko kulondola, kulondola ndendende. Ine ndikulingalira akazi aang'ono okongola Achimoabu amenewo anali okongola kwenikweni.

<sup>127</sup> Ine ndiri ndi uneneri ndawusiya kwathu, limodzi la masiku awa ine ndidzawuwerenga iwo. Ndipo inu mumadabwa chifukwa chimene ine ndimamenyera akazi momwe ndimachitiramu. Zaka sarte zapitazo. . . Ine ndiri ndi PAKUTI ATERO AMBUYE! Zaka sarte zapitazo pamene ine ndinalowa mu utumiki, Iye anandiuza ine kuti kupanikizika kwa akazi kudzabwera mwadama kwambiri ndi kowerengeredwa mmasiku otsiriza iwo adzakhala chinthu chodetsedwa kwambiri pa dziko lapansi. Kulondola! Iye anaziyambitsa izo pachiyambi ndipo Satana akumugwiritsa iye ntchito kumapeto. Ndipo taonani zomwe zikuchitika, muwone kudutsa mu zakazi. Anati, “Iye adzapitiriza kudzivula yekha.” Ndipo anati, “Padzakhala gulu laling'ono kwambiri, la Osankhidwa kumene omwe anakonzedweratu, ati adzazembe zimenezo.”

<sup>128</sup> Pamene masomphenya amenewo anabwera, izo zinandidandaulitsa ine. Ine ndinaganiza, “Akazi. . .” Ine ndinatembenezira mmbuyo mu Baibulo ku Yesaya, ine

ndikukhulupirira mutu wa 5, ndipo Ilo linati, “Nthambi yomwe yathawa kuchoka...ana aakazi a Zion, mu tsiku limenero adzakhala okongola kwa Ambuye.”

<sup>129</sup> Mkazi anandilemba ine funso tsiku lina, iye anati, “M’bale Branham!” Kapena, ayi, anali mwamuna, mtumiki. Iye mwina wayima pano mmawa uno. Iye basi ndiwochokera ku Ohio. Ndipo iye anati, “Ife tikufuna kuti tizinena chinthu chomwecho chimene inu mumachita, koma ife tinapeza chinachake pa matepi anu chimene sichiri cholondola.” Chotero Billy anabweretsa kalatayo kwa ine. Anati, “Chinachake pa matepi anu,” anati, “ndi chotsutsana kwambiri, M’bale Branham, ku Mawu a Mulungu. Ndipo ife tikufuna kuti—ife tikufuna kunena chinthu chomwecho.” Anati, “Funso limodzi limene ine ndikufuna kuti ndinene kwa inu, ndiro Akorinto Woyamba, mutu wa 11, ndipo ilo likunena kuti za chophimba kumutu kwa akazi, ndipo amuna asakhale ndi chophimba.” Anati, “Ife timakhulupirira zimenezo. Azimayi azivala zipewa mu tchalitchi, ndipo amuna azivula zipewa zawo mu tchalitchi.” Anati, “Ife timakhulupirira zophimba kumutu zimenezo, ndi zina zotero.” Ndipo anati, “Ndiye funso lina ndi lakuti anthu amabwera kwa ife ndi kunena kuti Mngelo wa Ambuye amayankhula chirichonse kwa inu. Mawu aliwonse amene inu mumayankhula amachokera kwa Mngelo wa Ambuye. Ndipo, M’bale Branham, ndizovuta kwambiri kumenyana ndi chinachake chonga icho,” anati, “mu mpingo wanga.” Anati, “Ife tikufuna kuti tizinena chinthu chomwecho. Tsopano, M’bale Branham, kodi inu simukukhulupirira kuti inu munali mu kulakwitsa pang’ono pamenepo?”

<sup>130</sup> Ine ndinalamba mobwenzera, “M’bale wanga wofunika, ine sindiri mu kulakwitsa. Akorinto Woyamba, mutu wa 11, anati mkazi aziphimba mutu wake, ndi chifukwa chake. Ndiye ndime ya 15 inati tsitsi lake lalitali linapatsidwa kwa iye kuti likhale chophimba, osati chipewa.” Mzimu wa Chikatolika uwo walamulira mpingo motalika kwambiri. Tsitsi lake lalitali ndi chophimba chake. Kodi chirengedwe pachokha...

<sup>131</sup> Ndipo taonani, ndipo kenako funso linadzabwerera, ninawake anandifunsa ine nthawi ina yapitayo... Ndizifotokoza izo ndikafika pa zimenezo. Iye anati, “Chabwino, Baibulo linanena kuti iye akuyenera kukhala ndi tsitsi lalitali chifukwa cha angelo. Kodi angelo angakhale ndi chochita chanji ndi mkazi?”

<sup>132</sup> Ine ndinati, “Kodi mngelo ndi chiyani? Ndi mtumiki.” Kodi Paulo akunena chiyani? Ngati mtumiki woona, mngelo wochokera kwa Mulungu adzabwera pamenepo, inu kulibwino mudzakhale ndi tsitsi lalitali. Iye adzachitsutsa chinthucho. Uko nkulondola. Ndi angati ali...akudziwa kuti mngelo ndi mtumiki? Kulondola ndendende. Mtumiki wotumidwa kuchokera kwa Mulungu adzachitsutsa icho. Anati, “Inu

kulibwino mukhale ndi tsitsi lalitali, chifukwa cha angelo.” Atumiki amenewo otumidwa kuchokera kwa Mulungu akadzabwera pamenepo, adzachitsutsa chinthu chimenecho. Inde, ndithudi, chifukwa, mtumiki weniweni wochokera kwa Mulungu, mngelo ndi wolumikizidwa ndi Mulungu, ndipo Mawu Ake sangalephere. Ndizo kulondola ndendende. Paulo Woyera ananena pamenepo, kuti ngati ngakhale Mngelo wochokera Kumwamba atabwera kudzaphunzitsa chinachakenso, mulole iye akhale wotembereredwa. Uko nkulondola. Tsopano ife tikupeza kuti izo ndi zoonna, iye akuyenera kukhala ndi tsitsi lalitali, ndicho chophimba chake.

<sup>133</sup> Koma ine ndikulingalira akazi owoneka bwino Achimoabu awa anali okongola kwambiri, iwo akuyenera kuti anazimangirira zina monga ma Yezebeli amakono a lero. Koma, komabe, si akazi onse! Ine ndikuganiza kuti mkazi amene ali weniweni ndi ngale. Mulungu alemekezeke chifukwa cha mkazi weniweni. Inu ndi adzakazi a Mulungu. Koma mkazi weniweni ali ngati mwamuna weniweni, iwo amatsatira Mawu a Mulungu mosalabadira chimene mdierekezi akunena, kapena chinthu chabodza chirichonse.

<sup>134</sup> Ndi kumati, “Abusa athu ananena kuti ndi zabwino kuchita *ichi*.” Ine sindikusamala zomwe abusa anu anena. Ngati izo ziri zotsutsana ndi Mawu a Mulungu, musiyere mawu awo akhale bodza, ndipo musunge Mawu a Mulungu. Sindikusamala ndi chipembedzo chanji kapena chomwe iye ali, ngati iye ali ndi chirichonse choti anene pa izo, muwuzeni iye kuti ayang’ane mu Mawu a Mulungu. Kulondola ndendende.

<sup>135</sup> Oh, momwe tingatsikire mmusi ndi kumuwona Mulungu akuwalekanitsa iwo. Ife tikuyenera kuyima miniti yokha. Ine ndiri ndi Malemba ena apa amene ine ndikufuna kuti ndingowalambalala iwo, kuti ndifike, ndifulumire kuti ndifike ku mapeto. Kenako pamene . . . chinachitika ndi chiyani pamene Iye anatenga malo kumeneko, pamene akazi Achimoabu? Mulungu ankayenera kuti awalekanitse iwo kachiwiri. Kodi Iye anachita chiyani?

<sup>136</sup> Kenako kunadzabwera Yesu. Tsopano kumene ife tikubweraku ndi kwinakwake. Kenako kunadzabwera Yesu, chifaniziro chowonetseredwa cha Mulungu, mbewu ya mkazi, yokhalitsidwa pakati ndi Mulungu Mwiniwake. Womanga wamkulu anadzimangira Yekha thupi. Iye sankayenera kubwereka matabwa aliwonse kwa aliyense, kwa mkazi kapena mwamuna. Iye anadzimangira Yekha nyumba. Oh, mai!

<sup>137</sup> Ine ndikuganiza za Stefano pa tsiku lija pamene iye anayima, anati, “Inu osadulidwa mu mtima ndi mmakutu inu, inu owuma makosi. Inu nthawizonse mumawukaniza Mzimu Woyera. Monga makolo anu ankachitira, inunso mukutero!” Anati, “Solomoni anamumangira Iye nyumba, koma

Wammwambamwamba Kwambiriyo samakhala m'nyumba zomangidwa ndi manja, koma thupi Inu mwalikonza.”

<sup>138</sup> Sankayenera kuti akabwereke matabwa aliwonse kulikonse. Ahebri, mutu wa 11, ine ndikukhulupirira mu ndime ya 2 kapena ya 3, amanena kuti “Dziko linapangidwa ndi Mawu a Mulungu, zinthu zimene zinapangidwa kuchokera ku zinthu zosawoneka.” Mulungu anangoti, “Mulole pakhale,” ndipo apo panali. Iye sanasowe kuti achite kupita ndi kukati, “Bambo Mwezi, kodi inu mungandibwerekeko Ine matabwa pang’ono? Bambo Nyenyezi, kodi inu mungandipatseko Ine kasiyamu wina?” Mulungu samachita zimenezo.

<sup>139</sup> Iye sanachite kusowa kunena kuti, “Mariya, iwe undibwerekeko Ine dzira, Ine ndikufuna kuti ndipange thupi kuti Ine ndidzakhoze kudzakhalamo mmenemo.” Mulungu Mlengi anayankhula, ndipo iye anali mayi nthawi yomweyo. Iye sanali mayi, iye anali mkazi chabe atanyamula Mbewu Yake. Uko nkulondola. Kumbukirani, iye sanali amayi a Yesu. Dziko linanena choncho. Ndipezereni ine malo amodzi mu Lemba pamene Iye anamutcha iye amayi. Tsopano bwererani ku Mawu. “Amayi a Mulungu,” manyazi pa inu. Mukuona?

<sup>140</sup> Tsiku lina panali anthu ena ananena kwa Iye, anati, “Amayi anu ali panja akukufunani Inu.”

<sup>141</sup> Iye anati, “Amayi Anga ndi ndani?” Anayang’ana pa ophunzira Ake, anati, “Two amene amachita chifuniro cha Atate Anga ndiwo amayi Anga.”

<sup>142</sup> Iye sanali amayi Ake, iye anali chofungatira. Mulungu akanatha kugwiritsa ntchito chinachakenso, koma Iye ankafuna kutenga chotsikitsitsacho ndi kuwonetsera chimene Iye akanakhoza kuchita ndi icho. Kuchikweza icho, kupanga chinachake kuchokera popanda kanthu, ameneyo ndiye Mulungu.

<sup>143</sup> Fanizo lowonetseredwa linadzabwera, Yesu, Mmodzi wangwiroyo, Mmodzi wokonedwayo, wokongola kwambiri mwa teni sauzande, Kakombo wa Mchigwa, Duwa la Sharoni, oh, Nyenyezi ya Mmawa. Iye anali chiyani? Kodi Iye anabwerera chiyani? Mvetserani mwacheru tsopano. Kudzakhazikitsanso umodzi pakati pa Mulungu ndi munthu. Oh, kodi inu mukuziwona izo, m’bale?

<sup>144</sup> Nsanja zawo zonse za Babelo ndi zinthu zawo zina zonse kumbuyo uko sizinagwire ntchito. Zipatso zawo zonse za m’mindanda ndi zina zonse zinamukwiyitsa Mulungu. Chotero Mulungu anadzatsika ndipo anadzayembekezedwa m’mimba ya mkazi, mwa Iye Mwini Wake, anadzipangira Yekha thupi, ndipo anadzakhala Emanuele, Mulungu nafe; osati Myuda kapena Wamitundu, koma Mulungu. Iye sanali Myuda, Iye sanali Wamitundu, Iye anali Mulungu. Ndipo Amitundu anali mochulukira basi kwa Iye pa nthawi iliyonse, kokha Iye



ankayesera kuti alekanitse Myuda kwa fuko. Iye anayesetsa kuchita chirichonse kuti abwezeretse izo, ndipo njira yokhayo yomwe Iye akanakhoza kudzikhazikitsira izo inali kubwerera kwa munthu monga Iye analiri pachiyambi. Umo ndi momwe ziriri lero, kwa munthu payekha. Osati kwa chipembedzo, osati kwa bungwe, osati kwa gulu la anthu; koma kwa munthu payekha. Zindikirani, kudzakhazikitsanso umodzi pakati pa Mulungu ndi munthu.

<sup>145</sup> Iye anali nsembe ya-tchimo yeniyeni. Nkhosa, mbuzi, ndi zina zotero, sizikanakhoza konse kuchotsa tchimo. Koma moyo. . . Chifukwa pamene nsembe yaphedwa ndipo moyo wa mwanawankhosa, chinthu chosolakwa kwambiri, sukanakhoza kuti ubwererensho, moyo umenewo, pa wokhulupirira, chifukwa iye anali munthu, wokhala ndi solo, ndipo nkhosa siimakhala ndi solo.

<sup>146</sup> Mwaona, palibe chimene chimakhala ndi solo koma munthu. Mulungu anayika. . . Iye ndi mawonekedwe achinyama, izo nzoona, koma Iye anayika solo pa iye. Icho ndi chimene chinamupangitsa iye kukhala wosiyana ndi nyama. Iye ankadziwa chabwino ndi choyipa pamene solo yake inabwera pa iye. Koma iye. . . Kumbukirani pamene Mulungu anamulenga munthu mu chifanizo Chake Chomwe, ndipo kenako iye anadzakhala solo yamoyo. Mwaona, iye anadzakhala chimenecho, akudziwa chabwino ndi choyipa.

<sup>147</sup> Tsopano zindikirani. Koma tsopano, mu ichi, Yesu anabwera ndipo Iye anali Mulungu. Osati kokha moyo wa munthu wina ukhoza kubwerera pa munthu wina, koma Moyo womwewo wa Mulungu, kumupanga iye mwana wa Mulungu, kumubwezeretsa iye mmbuyo mu chilumikizano chomwecho chimene iye anali kusanachitike kugwa. Tsopano tikupeza umodzi weniweni.

<sup>148</sup> Anthu, winawake amanena kwa ine, “M’bale Branham, kodi sindinu wa umodzi?” Osati bungwe la Umodzi. Koma ine ndi wa umodzi ndi Khristu, mwaona, koma osati Umodzi wa bungwe.

<sup>149</sup> Iye analipira ngongole ya tchimo. Tsopano, kuti apeze umodzi pakati pa Mulungu ndi munthu, Yesu sakanakhoza kuchita izo pokhapokha ngati Iye akanakhala kuno mu thupi la mnofu. Chotero Iye ankayenera kukhala nsembe ya tchimo yathunthu kuti adzachotse cholakwa cha wokhulupirira, mwaona, kudzachotsa icho kuti Mzimu Woyera udzakhoze kubwera mwa munthu, ndi kudzamupanga munthu ndi Mulungu kukhala umodzi kachiwiri. Mwaona, pankayenera kukhala chinachake choti chidzakhazikitsenso.

<sup>150</sup> Tsopano, ndi chiyani chikanadzakhazikitsanso? Pamene lamulo la Mulungu lakwaniritsidwa. Kodi Mngelo akanakwaniritsa icho? Iye alibe magari. Kodi Mulungu akanakwaniritsa icho? Iye analibe magari. Ndipo Mulungu anasandulika thupi ndi magari ndi cholinga chakuti Iye

adzakhoze kulipira ngongoleyo molondola ndi kudzachotsa tchimo, chifukwa ndiyo njira yokhayo. Nsanja za Babelo zikuwalekanitsa iwo pa dziko lapansi, china chirichonse, mabungwe ndi zinthu zinali zitalephera mwa njira iliyonse, iwo amasakanikirana pamodzi, dziko ndi china chirichonse, koma uku kukanakhala kulekana kwathunthu. Ulemelero!

<sup>151</sup> Tsopano ine ndikumverera mwachipembedzo. Chabwino, ine ndikumverera ngati ine ndikhoza kutenga mutu wanga tsopano ndi kuyamba kulalikira pakali pano. Ndikungotenthetsetwa tsopano mpaka pomwe ine ndingakhoze kuyambira pomwe pano, ndipo nthawi yakwana yoti ine ndiyime. Uhm! Mwinamwake ine ndidzatsirizitsa izo nthawi ina, umodzi wa Mulungu ndi munthu. Kodi inu mukumvetsetsa? Onse amene akumvetsa, nenani “Ameni.” [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi].

<sup>152</sup> Mwaona, ndiyo njira yokhayo imene munthu akhoza kubwerera mu chikhalidwe chake chapachiyambi kachiwiri, ndi kuti chilango cha tchimo chimenecho chiripidwe. Chilango cha tchimo ndi chiyani? Imfa. “Mphotho ya tchimo ndi imfa.” Ndipo Mulungu anati, “Tsiku limene inu mudzadya umenewo, tsiku limene inu mudzachte mchitidwewo, ndiro tsiku limene mudzafe.” Ndipo pamene izo zinatero, izo zinaswa ubale wake, chijanano ndi chirichonse kwa munthu, ndipo sakanabwereranso mpaka chilangocho chitalipiridwa. Ndipo panalibe aliyense woyenera kulipira icho, pakuti aliyense anagwa ndi munthu, chifukwa cholengedwa chirichonse chiri panso pa munthu, ndipo iye anali wakugwa. Ulemelero! Oh, m’bale!

<sup>153</sup> M’bale Mac, ine sindinakuwoneni inu mutakhala pamenepo, Mulungu akudalitseni inu. Ife timakhulupirira izi, M’bale Mac. “Kubwera panso pa chilango cha imfa.” M’bale Mac kuno anali m’busa kuno ku kachisi pamene ine ndinkachoka. Eya. Tsopano, wa Baptisti wina wabwino wakale, Missionary Baptist kumusi kumeneko amene analandira Mzimu Woyera. Mukuona? Zindikirani tsopano, mubwere mu umodzi ndi Mulungu.

<sup>154</sup> Tsopano, pamene ife tiwona izi, kuwona kuti chilango chikuyenera kulipiridwa, ndipo zindikirani, mawonekedwe apamwamba kwambiri a moyo wa chinyama ndi munthu, ndipo munthu anagwa, iyemwini. Chotero munthu mmodzi angampulumutse bwanji mzake? Izo zinatengera Mulungu. Ndipo Mulungu, mu Mzimu, sakanakhoza kufa. Chotero, “Mulungu ankayenera kudzibweretsa Yekha motsikirapo pang’ono kuposa Angelo,” Ahebri mutu wa 1, ndime ya 1. Anachita kudzipanga Yekha wotsikirapo kuposa Angelo kuti adzatenge imfa, kuti adzalipire chilango, kuti adzabweretse umodzi pakati pa munthu ndi Mulungu kachiwiri, kuti Mzimu Woyera ukhoze kudzabwereranso.

<sup>155</sup> Ngongole ya tchimo inalipidwa. Yesu ankayenera kuchita izi kuti adzatumize a—a—Mzimu Woyera kubwerera pa, kuti udzayanjanitsenso anthu monga zinakhhalira mmunda wa Edeni. Ngongoleyo inalipiridwa pamene Yesu anafa. Izo zinakhazikitsa izo. Ameni, m'bale! Ngati ine ndingakhoze kokha kuzifikitsa izo kuti zilowerere mkati, mwawona. Ngongoleyo yalipiridwa. Aleluya kwa Mwanawankhosa! Ngongoleyo yalipiridwa. Ndipo mwamuna ndi mkazi aliyense amene akundimva ine mmawa uno, kapena ati adzandimve ine pa tepi, chilango chanu chinalipiridwa. Inu musati musamakhlupirire Mawu a Mulungu kachiwiri. Bwererani ku Mawu! Musakhlupirire zimenezo. . .Iye anali Mawu. Ulemelero! Ine ndikumverera ngati ndifuule, moonadi ine ndikutero. Chilango chalipiridwa. Zonse zatha. Nzosadabwitsa Angelo anafuula ndi kuyimba, nyimbo za Kumwamba zikumveka. Inde, bwana, nkhoa zotayika zinapezedwa! Chitetezero chinapangidwa kuti iye abwezeretsedweno kachiwiri, madzi olekanitsa, Mawu a Mulungu amene amamutsuka iye ku kusaeruzika kwake, pamene Mawu anafa mmalo mwanga ndipo anawukitsidwa kachiwiri ndi kudzakhala apamwamba mmoyo wanga, mu mtima mwanga. Ameni. Chilango chinalipiridwa! Izo zinatha. Ndife owomboledwa.

<sup>156</sup> Osati mwa mpingo wa Katolika; ngakhale ife ndi akatolika olondola, katolika wa utumwi. Inde, bwana. Osati Roma Katolika ndi miyambo yawo, iwo amakana Mawu awa chifukwa cha miyambo yawo; chirichonse ndi miyambo yanu, osati Mawu. Amethodisti, Abaptisti, manyazi pa inu, okonda kusaeruzika kuposa okonda Mulungu. Okonda zosangalatsa, ofunafuna dziko, zosangalatsa, okupha nkhumba pofuna khola. Mdierekezi akutumiza zida zake kunja uko akutsamwitsira zinthu zimenezo pansu panu monga Satana anachitira mmunda wa Edeni. "Chabwino, atumiki athu onse ali ndi maphunziro. Iwo ali ndi Ph.D., LL.D." Izo sizikutanthauza kanthu. Kumakana Mawu amenewo, iyo ikadali njomba ya mdierekezi. Ine ndatsimikizira izo kwa inu mwa Mawu mmawa uno, zikhale kwa inu kuyambira tsopano.

<sup>157</sup> Ophunzira, ngakhale akuyenda ndi Yesu, analibe umodzi. Iwo analibe mgwirizano uliwonse. Ayi, iwo ankatsutsana, "Ndani ati adzakhale bishopu zikatha izi. Ndani wamkulu pakati pathu?" Iwo samakhoza nkomwe kumukhlupirira Yesu. Iwo samakhoza kumumvetsa Iye. "Inu mukuyankhula mmikuluwiko. Tiwuzeni ife momveka chimene Inu mukutanthauza." Panalibe mgwirizano pakati pa Yesu ndi ophunzira, kapena ophunzira kwa Yesu, ndi ophunzira pakati pa wina ndi mzake.

<sup>158</sup> Ziribe kanthu, izo zizikusonyezani inu, m'bale. Mvetserani mwatcheru tsopano, ine ndikufuna izi zimamatire kwenikweni pansu mu mtima mwanu. Mukuona? Mulungu ali ndi dongosolo.

Kunja kwa dongosolo limenero, ine sindikusamala ndi nzeru zochulukira bwanji ziri kumbuyo kwake, ndi mamillioni abwino angati a madola a nyumba, ndi masukulu angati a fioloje, ndi amuna oyera angati ndi oyera *ichi*, ndi oyera, oyera, oyera, sizimapanga kusiyana kulikonse nkomwe, ngati Mawu amodzi a Baibulo la Mulungu akanidwa, izo ndi za mdierekezi. Tsopano, ine ndatsimikizira izo kwa inu mwa Mawu olembedwa a Mulungu, kuchokera ku Chatsopano kupita ku Chipangano Chakale, ndipo ndimubweretsa iye mpaka tsikulo ngati mungokhala ndi ine maminiti angapo.

<sup>159</sup> Ophunzira amene ankayenda dzanja ndi dzanja ndi Yesu, ankagona ndi Iye, ankadya ndi Iye, anawona zozizwitsa Zake, ndipo anayanjana ndi Iye, moyandikira monga m'bale aliynse akhoza kukhalira, ndipo komabe iwo analibe izo. Iwo sanali oyenera kulalikira Uthenga. Yesu anati, "Musati mukalalikire nkomwe, musati mukayesere nkomwe. Inu mukadikirire kumtunda uko ku mzinda wa Yerusalemu. Ine nditumiza lonjezo, limene laperekedwa kwa inu, pa inu. Ilo lidzakugwirizanitsani inu pamene." "

<sup>160</sup> "Tsopano, Atate, Ine ndikupemphera kuti iwo adzakhale mmodzi monga Inu ndi Ine tiri Mmodzi. Ndipo Ine . . ." "Monga Atate Anga anandituma Ine kuti ndidzalalikire Uthenga, chomwechonso Ine ndikukutumani inu."

<sup>161</sup> Ndipo Atate omwewo amene anamtuma Mwanayo, anabwera mwa Mwanayo. Mgwirizano monga Mmodzi. Iye anati, "Ngati Ine sindichita ntchito za Atate Anga, ndiye musandikhulupirire Ine. Koma ngati ntchito Zanga zimene Ine ndizichita zikuyankhula mokweza kwambiri, ndinu ogontha kwenikweni, osayankhula ndi akhungu ngati inu simukuziwona izo." Oh, m'bale, psyii! Anati, "Inu achinyengo! Inu mumakhoza kuzindikira nkhope ya thambo, koma zizindikiro za nthawiyo inu simungakhoze kuzindikira. Ngati inu mukanandidziwa Ine, inu mukanadziwa tsiku Langa. Yesaya analankhula bwino za inu. Inu muli ndi makutu, ndipo ndinu ogontha chotero mwakuti inu simungakhoze kumva. Maso, ndipo akhungu chotero mwakuti inu simungakhoze kuwona!"

<sup>162</sup> Mwabwino mtumwi Paulo anati, "Mmasiku otsiriza iwo adzakhala ndi mawonekedwe aumulungu ndi kukana Mphamvu yake," ndipo Lemba pa Lemba, zomwe zikanati zidzachitike mu mabungwe awa mmasiku otsiriza. Ndiye iwo amadabwa chifukwa chimene ine ndimafuwulira motsutsa kachitidwe kopangidwa ndi anthu ka mdierekezi kameneko. Kuwaona ana ofunika awo atatsogoleredwera kunja uko ngati nkhoa zopita kokaphedwa. Atulutseni iwo, Ambuye!

<sup>163</sup> Inde, ophunzira analibe mgwirizano. Iwo amalephera kumumvetsetsa Yesu. Iwo anati, "Ah, ndani angamvetse zinthu zimenezi?" Mwaona, Mulungu anali asanabwerebe

mwa iwo apobe. Iwo anali ongoyanjana mu chiyanjano. Iwo ankangoyanjana ndi Iye. Amenewo ndi anthu abwino ambiri lero. Iwo sankamwa, kunama, kuba, kalikonse, koma iwo analibe umodzi umenewo wa Mulungu. Iwo sanali mmodzi ndi Mulungu apobe. Mwawona, iwo sakanakhoza kukhala. Oh, iwo ankachita zozizwitsa. Iwo ankatulutsa ziwanda. Izo si a—izo si a . . .

<sup>164</sup> Ine ndinawerenga nkhani mu pepala tsiku lina ya izo, ya kutulutsa ziwanda. Anthu amati, “Oh, m’bale, ine ndikukuuzani inu, ndi zimenezo.” Izo si zimenezo! Munthu amene amatulutsa mdierekezi ndi kukana Mawu a Mulungu, ndi wabodza. Inde, bwana. Iye akuti amatulutsa ziwanda. Iwo amadzinenera kuti amachita zimenezo. Iye sangachite izo ngati iye alibe Mawu a Mulungu. Yesu ananena chomwecho.

<sup>165</sup> Tsopano, kenako kunadzabwera Pentekoste, Mulungu anawapanga iwo mmodzi kenanso. Oh, mai! Kenako iwo anadzakhala ndi umodzi ndi Mulungu. Mulungu anadzakhala mwa iwo. Tsopano, Machitidwe, ngati inu mukulemba zimenezo, Machitidwe 4:32, Baibulo linanena kuti “Iwo anali ndi mtima umodzi, solo imodzi, ndi malingaliro amodzi.” Oh, m’bale. Chifukwa chiyani? Iwo anali atabwezeretsedwa ku chapachiyambi kenanso. Chinthu chokhacho chimene iwo anasiya kuti chitayidwe chinali mzinda wakale, kapena iwo ankakhala kuno, thupi lakale lotchedwa mzinda kapena kachisi, limene iwo ankakhalamo kuno, lomwe linkayenera kuvunda, chifukwa ilo likuyenera kufa ndi kuvunda. Koma mu mzimu ndi moyo, ndi mu cholinga ndi masomphenya, ndi chirichonse, iwo anali amodzi ndi Mulungu.

<sup>166</sup> Oh, Adamu, mzanga wokhumudwa, usamulole Satana kuti akuwuzenso iwe bodza lake kachiwiri. Usalole kuti izo zichitike. Usati umulole Satana akuwuze iwe kuti Mawu samatanthauza zomwe Iwo amanena. Uko nkulondola. Mawu amatanthauza . . . Eya, kuno osati . . .

<sup>167</sup> Ine ndimayankhula pa ubatizo wa Dzina la Yesu Khristu. Uko nkulondola, vumbulutso la izo linabwera. Ndicho Choonadi. Koma kodi gulu la anthu linachita chiyani? Anazisonkhanitsa izo pomwe pano ndi kuyika chipembedo kuchokera mmenemo, anapanga nsanja ina ya Babelo. Chinthu chomwecho, anachiponyera icho mmenemo. Ndithudi. Luther anachita chinthu chomwecho. Wesley anachita chinthu chomwecho, John Smith anachita chinthu chomwecho, Alexander Campbell anachita chinthu chomwecho. Pentekoste inachita chinthu chomwecho. Mulungu amachita ndi munthu payekhapayekha akusunga Mawu Ake. Dongosolo lokhalo la Mulungu lobweretsa okhulupirira kwa Iyemwini, mu umodzi woona, ndi kulandira Mzimu Woyera. Ndiye apa pali momwe . . .

<sup>168</sup> Inu mukuti, “Chabwino, M’bale Branham, ine ndinayankhula mmalirime. Ndinafuula. Ndinachita *ichi*.”

Ngati inu mukadali ndi mzimu wa mtundu umenewo ndi kumakana Mawu a Mulungu, inu mulibe Mawu a Mulungu mwa inu, inu mulibe Mzimu. Ngati inu mukhala pansu ndi kumamvetsera Choonadi chikulalikiidwa, ndi kuchiyang'ana Icho mu Baibulo ndi kuwona Ndicho Choonadi, ndipo kenako nkukana kuchichita icho, umenewo si Mzimu wa Mulungu. Ine sindikusamala ndi mochuluka bwanji momwe inu munayankhula mmalirime, mochuluka bwanji momwe inu munafuula, mipingo yochuluka bwanji yomwe inu mwakhalamo, kapena ndi kangati inu munabatizidwa, kapena china chirichonse. Mawu ndi Choonadi. Ndicho chimene chimatsimikizira choonadi. Ngati inu muli ndi zoonadi zina zonsezi ndipo kenako ndi Mawu, ameni, ndiye inu mumadziwa kuti inu mukubwera kwanu.

<sup>169</sup> Angakhoze. . . Mulungu yemweyo amene analemba Baibulo angakhoze bwanji kutembenuka ndi kudzalowetsa mmalo chinachake mmalo mwa Mawu Ake? Inu anthu Achikatolika amene munanena kuti Petro anayikidwa mu tchalitchi chanu, ndipo mzimu wake umakupatsani inu ufulu wochotsa machimo ndi zinthu, Petro akanakhoza bwanji, Myuda, kupirira ndi kukhala ndi mafano mu tchalitchi? Petro akanakhoza bwanji kukana nkomwe kunena kuti ubatizo wa Mzimu Woyera ubwere, ndipo iye anayankhula mmalirime, ndi zinthu zonse zamphamvu izo iye anazichita, ndi kutembenuka mozungulira ndi kudzati tengani kokulumunya kakang'onoko, ndipo Mulungu ali mu kokulumunya kameneko? Oh, ndi umbuli, umbuli wauzimu!

<sup>170</sup> Chabwino, tsopano, inu Achiprotestanti chinthu chomwecho, mumayenda ndi kugwirana chanza ndi mlaliki, ndi kudzanena kuti, "Ndikumuvomereza Yesu ngati Mpulumutsi wanga," ndi kubwerera mmbuyo ndi kukakhala mtundu uliwonse wa moyo kuchokera mu izo, ndi kumapitirira kumakhala ndi dziko. Nsanja ina ya Babelo.

<sup>171</sup> Tikufika kumapeto tsopano. Penyani. Mulungu anatomiza Mzimu Woyera, ndipo Mzimu Woyera ndi Mulungu Mwiniwake. Iye ndi Mmodzi yemwe ati adzapange umodzi pakati pa Mulungu ndi munthu. Tiyeni tifufuze. Tsopano tiyeni. Tsopano ine ndikufuna chidwi chanu chosagawanika kwa maminiti asanu otsatira kapena choncho. Penyani.

<sup>172</sup> Munthu pansu pa dongosolo la mdierekezi wayesetsa kuti awupange chipembedzo mpingo kukhala mu umodzi. Iwo ayesetsa kupanga bu- . . . kuwuphunzitsa mpingo mu umodzi, inu mukudziwa zimenezo, kudzera mu maphunziro, kudzera mu chipembedzo. Iwo akuyesetsa pakali pano, World Council of Churches, kumapitirira kuyesetsa kubweretsa Akatolika onse ndi Achiprotestanti pamodzi ndi kuwapanga iwo mmodzi. Ndi chiyani icho? Dongosolo la mdierekezi!

<sup>173</sup> Inu mukuti, "Ndiwe wamng'ono kwambiri kuti uzinena

zimenezo.” Ndine wamng’ono kwambiri, koma Mawu a Mulungu wanga ndi aakulu kwambiri, ine ndikuwuzani inu zimenezo. Miyamba ndi dziko lapansi zidzachoka, koma Iwo sadzatero. Si iye amene akunena izo, ndi Iye amene—Iye amene—Iye amene ananena izo poyamba. Ine ndikungonena zimene Iye ananena, ine ndikuvomereza Mawu Ake.

<sup>174</sup> Ziri pansi pa mdierekezi! Izo zatsimikiziridwa mu Mawu apa, mmawa womwe uno pamaso panu, kuti izo ndi za mdierekezi. Aliwonse a mabungwe amenewo ali. Amuna, pansi pa dongosolo la mdierekezi, amayesetsa kuwapanga chipembedzo anthu kukhala umodzi.

<sup>175</sup> “Nonsenu mubwere mudzajowine Assemblies of God. Mudzajowine Umodzi. Mudzajowine Mpingo wa Mulungu. Mudzajowine Methodisti. Ife tonse ndi amodzi.” Inu gulu la achinyengo, okhala nawo mawonekedwe aumulungu ndipo nkumakana Mphamvu yakeyo. Ndipo Mawu a Mulungu akagwedezera pamaso panu pomwe, ndipo inu mumachita mantha kukumana nawo Iwo. Bwanji Mulungu sakudziwonetsera Yekha ndiye, ngati inu muli ndi Mulungu? Chifukwa chiyani simukuchita ntchito za Mulungu? Inu mungakhale bwanji ndi mawonekedwe amenewo, ndi kumapita pamenepo ndi kumamukana Iye, ngakhale kudzitcha ntchito zenizeni za Mulungu Bezezebule? Izo zikusonyeza, inu gulu lophunzira la mamembala a mpingo! Yesu anati, “Inu ndinu a atate wanu, mdierekezi!” Kulondola! Ine ndikutsimikiza kuti inu mukumvetsa zomwe ine ndikutanthauza. Ndithudi. Chifukwa chiyani wina sakumanizana nawo Iwo? Inu mukudziwa Mulungu ali kuseri kwa Iwo. Mulungu adzasuntha ndi Mawu Ake.

<sup>176</sup> Munthu amachita zimenezo, izo zimamanga nsanja ina ya Babelo. Kodi iye amachita chiyani? Iwo amayesetsa kusonyeza. . . Tayang’anani mu World Council of Churches iyi tsopano. Anglican, Roma Katolika, Amethodisti, Apresbateria, Apentekoste, ndi onse a iwo alumikizana pamodzi, Christian Science, ndi zipembedzo zambiri zomwe zimakana ngakhale kubadwa mwa namwali, zomwe zimakana Umulungu wa Yesu, kumupanga Iye anthu atatu, kuyesera kumapembedza milungu itatu, kumakana kubadwa mwa namwali. Ena a iwo amakana Magazi. Ena a iwo amakana zozizwitsa Zake. Onse a iwo amatero, pafupifupi. Ndiye kenako—ndiyeno nkumayesetsa kuyanjanitsa zoterozo monga izo pamodzi, inu mungachite bwanji zimenezo? Ndi nsanja yopangidwa ndi anthu. Idzagwa monga Babelo anachitira.

<sup>177</sup> Koma Mulungu anati, “Osati mwa mphamvu, osati mwa kuthekera; ndi Mzimu Wanga, atero Ambuye. Umo ndi momwe Ine ndidzawugwirizanitsire Mpingo Wanga. Osati mwa bungwe, osati mwa maphunziro, osati mwa azafiolole; koma mwa Mzimu Wanga, atero Ambuye, Ine ndidzabweretsa

nkhosa Zanga pamodzi.” Oh, mai! Ndipo pamene Iye atero, chidzachitike ndi chiyani? Ndipo zizindikiro Zake zidzayikira umboni wa zomwezo. Umo ndi momwe Israeli akanakhoza kumanena, asanasakanizike ndi Moabu. Apo panali Lawi la Moto pa iwo. Inde, bwana. Kodi Iye adzachita chiyani? Iye adzachitira umboni, mtundu womwewo wa umboni. Koma atatha kulekanitsidwa ndi zina zotero ndi Mulungu, atalekanitsa umodzi wawo pakati pa iwo ndi Mulungu, ndipo nkudzalowana ndi Moabu ndi iwo, chigonjetso chonse chinalephera. Iwo anakhala mu chipululu kwa zaka forte zina, mpaka Mulungu anadzutsa gulu lina kuti lipite uko ndi kukamalizitsa dongosolo Lake. Ndizo ndendende zimene iwo anachita.

<sup>178</sup> Tsopano taonani. Koma pamene Mulungu awubweretsa mpingo pamodzi ndi Mzimu Wake, iwo adzakhala nazo zizindikiro Zake za Mulungu wamoyo pakati pawo. Zizindikiro za mtundu wanji? Pamene Mulungu anamulekanitsa Israeli kwa Igupto, Mulungu anampatsa Mose ndi Israeli chizindikiro cha Lawi la Moto. Nkulondola uko? Mneneri. Pamene Iye anamulekanitsa Abrahamu kwa Loti, apo panali Mngelo anabwera kwa iye, yemwe ankakhoza kuzindikira malingaliro ndi zolinga za mtima. Chizindikiro! Aleluya.

<sup>179</sup> Tsopano zipembedzo izi zomwe zinagwidwa mu mpingo uwu, kuyesetsa kupanga umodzi monga mu Igupto, monga kumusi mu—mu Edeni, ndi zina zotero, pansi pa chikoka chachikulu ichi chimene iwo ali.

<sup>180</sup> Koma, taonani, ine ndikufuna kuti ndikufunseni inu chinachake. Pamene Mulungu anamulekanitsa Israeli, Iye anawapatsa iwo chizindikiro Chauzimu, Lawi la Moto. Iye anawapatsa iwo mneneri. Kodi Iye anachita chiyani kwa Abrahamu? Kodi Iye amachita chiyani nthawi zonse? Ndisonyezeni ine mneneri wosankhidwa ndi Mulungu pakati pawo. Iye amawukhazikitsa mpingo Wake pamodzi mwa atumwi ndi aneneri ndi aphunzitsi ndi avangeli. Aleluya! Ndi zimenezotu. Mpingo, kachiwiri, monga Iye anayitanira Israeli atuluke. Ine ndinakuwuzani inu kuti ndibwereranso ku zimenezo. Inde, bwana.

<sup>181</sup> Panalibe aneneri osankhidwa ndi Mulungu pakati pawo, ayi, bwana, monga ankakhalira ndi Israeli ndi iwo. Ndi chiyani chimenecho? Nsanja ya mdierekezi kachiwiri.

<sup>182</sup> Tsopano, Kudzako kuli pafupi kwambiri, Kudza Kwachiwiri kwa Yesu, Iye akusonkhanitsa Osankhidwa Ake pamodzi. Ine ndikukhulupirira zimenezo. Oh, iwo adzabwera kuchokera Kummawa ndi Kumadzulo. Kumene kuli nyama, mphungu zidzasonkhanako. Oh, mai, ndi chiyani chimenecho? Iye ali ndi umodzi Wake, umodzi Wake woona, akudziwonetsera Yekha pakati pawo; kuchokera mu chipembedzo chirichonse, akubweretsa Osankhidwa Ake pamodzi kuchokera ku mitundu



yonse ya mipingo, kuchokera kulikonse, kuwatulutsa ana Ake, kumagwera mu mzere momwe ndi Mawu Ake. Chiyani?

<sup>183</sup> Tsopano, Kudza kwa Ambuye Yesu kuli pafupi kwambiri, kubwera kwa chiweruzo, Iye akuyitanira Osankhidwa Ake pamodzi mu umodzi ndi Iyemwini, ndi mtundu womwewo wa utumiki umene Iye anali nawo. Inu mukudziwa momwe ine ndinabweretsera Mibadwo ya Mpingo, kuno osati kale litali, za a—nsanja yaikulu imene inamangidwa, yotchedwa piramidi, koma mwala wapamutu sunayikidwepo pa iyo. Kumbukirani momwe Achilutera anabwerera, kenako a Wesley mwa ochepe, ndipo kenako mpaka ku Pentekoste. Ndipo tsopano chimene Iye akuchita, akuyitana kuchokera pamenepo. Kodi Iye anachita chiyani? Iye anayitana atuluke Osankhidwa, kuti akapange Achilutera; Iye anayitana atuluke Osankhidwa, kuchokera kwa Achilutera, kuti akapange Achiwesile; Iye anayitana atuluke Osankhidwa, kuchokera mu zimenezo, kuti akapange Achipentekoste; tsopano Iye akuwayitana Achipentekoste Osankhidwawo atuluke, kuti adzapange mwalawapamutu ubwere mu zimenezo. Utumiki wa mtundu womwewo ukugwera pa zimenezo, akuyitana ana Ake kuchokera ku zipembedzo zonse ndi mayendedwe onse a moyo.

<sup>184</sup> Kodi Iye wachita chiyani? Iye wawaikira iwo aphunzitsi owona, aneneri owona amene amakhala ndi Mawu Ake, Baibulo. “Nkhosa Zanga zimamva Liwu Langa,” anatero Yesu. Ngati ilo linali Liwu Lake nthawi imeneyo, ndi Liwu Lake tsopano. Chirichonse chotsutsana ndi Liwu limenero, si chakudya cha nkhosa. Iwo sangachitsatire icho. Oh, m’bale. Kuchokera Kummawa, kuchokera Kumadzulo, kuchokera mu chipembedzo chirichonse, kuchokera mu bungwe lirilonse, iwo abwera kuchokera Kummawa ndi Kumadzulo, akusonkhana pamodzi! “Tidzachita phwando ndi Mfumumu, kudya monga alendo Ake, ndi odala bwanji momwe amwendamnjira awa aliri! Kuwona nkhope Yake yopatulika ikuwala ndi chikondi cha Umulungu; odala otenga nawo gawo za chisomo Chake, ngati ngale mu korona Wake kuti aziwala. Yesu akubwera posachedwapa, mayesero athu pamenepo adzatha.” Aleluya! “Nanga bwanji ngati Ambuye wathu mphindi ino angabwere kwa iwo amene ali omasuka ku tchimo? Ndiye kodi zingakubweretsereni inu chisangalalo, kapena chisoni ndi kutaya mtima kwakukulu? Koma pamene Ambuye wathu mu Ulemelero adzabwera, ife tidzakomana naye Iye mumlengalenga.” Aleluya! Inde, bwana.

<sup>185</sup> Ndi chiyani chimenecho? Ndi aphunzitsi otumidwa ndi Mulungu amene ati azikhala ndi Mawu, kwa Mpingo weniweni, osati kusuntha kachidutswa kamodzi ziribe kanthu zomwe bungwe likunena. Iwo sali olumikizana ndi ilo. Aneneri; osati odzipangitsa-kukhulupirira, otchedwa choncho, koma mneneri weniweni amakhala ndi PAKUTI ATERO AMBUYE, ndipo amakhala pa dontho nthawi iliyonse.

Ndicho chimene Iye watumiza mu Mpingo Wake. Ndicho chimene Iye anati Iye akanadzachita. Amakhulupirira Mawu; osati kachikhulupiriro, osati miyambo, koma Mawu. Ndipo, pochita izi, Iye amadziwonetsera Yekha mwa iwo potsimikizira Mawu Ake, kupanga Moyo womwewo umene Iye anawukhala kamodzi, kuwukhalanso kachiwiri, kuwakwaniritsa Mawu Ake. Oh, mai!

<sup>186</sup> Mvetserani mwacheru. Akorinto Woyamba 4:20, amati, “Ufumu wa Mulungu ndi Mawu Ake opangidwa mphamvu.” Ngati inu mukufuna kuti mulembe zimenezo, Akorinto Woyamba 4:20. Ufumu wa Mulungu ndi Mawu a Mulungu opangidwa mphamvu. Kodi Ufumu wa Mulungu ndi chiyani? Uli mkati mwanu. Ufumuwo uli mwa inu. Ndipo pamene Mawu abwera mmenemo, kodi Mawu awa amayamba chiyani? Iwo amadziwina Okha kukhala mphamvu, kuwapangitsa Iwo kunena ndendende basi zomwe Iwo ananena.

<sup>187</sup> Inu simunganene “Iwo amanena *ichi*,” ndipo Iwo amanena Ichi, ndi kuwapangitsa Iwo kugwira ntchito. Inu mukuyenera kunena chinthu chomwecho chimene Iwo amanena. Izo zimapanga kuvomereza. Osati kumati, “Chabwino, Iwo apukutidwa pang’ono apa, ine ndikhala ndi nzeru zochulukirapo, ine ndikhala mu mayimidwe abwinoko cha apa.”

<sup>188</sup> Inu muzikhala ndi Mawu. Ndi zimenezotu, mwaona. Ndipo Iwo amawapanga Iwo amphamvu. “Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.” Yesu ananena, mu Yohane Woyera 14:12, “Ngati inu mukhala mwa Ine ndi Mawu Anga mwa inu.” Ayi, ine ndikupempha kukhululukira kwanu, izo si zimene Iye ananena pamenepo. Iye anati, “Iye amene akhulupirira mwa Ine, ntchito zimene Ine ndizichita iyenso adzazichita. Ngati inu mukhala mwa Ine ndi Mawu Anga mwa inu, inu mukhoza kupempha chimene inu mukuchifuna ndipo chidzachitidwa kwa inu. Ngati inu mukhala mwa Ine ndi Mawu Anga mwa inu.”

<sup>189</sup> Ndi chiyani chimenecho? Inu mukuyenera kuti mukhale ndi Mawu, mudziphe nokha. Ndine wokakamizika kuti ambiri a ife, abwenzi, talandira Mzimu Woyera, koma ife timangolandira Mzimu Woyera wokwanira mwa ife kuti utipangitse ife kufika pa malo amene ife sitimafuna kunama, sitimafuna kuba, sitimafuna kuchita chirichonse. Koma Mulungu akufuna kuti adzaze msempha uliwonse wa Mpingo Wake, Iye akufuna kuti adzaze kuganiza kwanu ndipo akufuna kuti adzaze malingaliro anu. Iye akufuna kuti adzaze chidutswa chirichonse cha inu, kungokupangani inu kwathunthu, wakufa kwathunthu kwa inumwini kapena ku kuganiza kwanu, basi wongodzipereka kwambiri mwa Mulungu mpaka Mawu Ake akungokhala moyo mwa inu. Inu osamadziwa kalikonse koma Mawu a Mulungu, kungokhala ndi Mawu Ake, Iwo ndi Moyo. “Mawu Anga ndi Moyo,” anatero Yesu. Iye anayika limodzi ndi iwo, aphunzitsi

okhulupirira Baibulo, aneneri amene amanena Choonadi, amene amanena, amawonetsera uneneri womwewo umene iwo akhala akuchita nthawi zonse kudutsa mu m'badwo. Kodi Iye wachita chiyani? Iye akudziwonetsera Yekha wamoyo pakati pawo, kutsimikizira Mawu Ake. Mawu ake, Ufumu wa Mulungu ndi Mawu a Mulungu opangidwa mphamvu.

<sup>190</sup> Pamene, zipembedzo izi zimadalira pa kulingalira kwa umunthu, pa kulingalira kwa umunthu. Mvetserani mwatcheru tsopano. Iwo . . . Ife sitiri oti tizidalira pa zolingalira za umunthu. Miyambo, mutu wa 3, ndime ya 5, inati, “Musamadalire pa kumvetsa kwanu kwanu.” Mukuwona? Musamachite zimenezo, ziribe kanthu momwe Mawu a Mulungu *akuwonekera* ngati.

<sup>191</sup> Inu mukuti, “Chabwino, izo zikuwoneka ngati ziri bwino mwanjira *iyi*.”

<sup>192</sup> Izo simomwe Iwo aliri. Iwo ndi Mawu a Mulungu, atengeni Iwo momwe Iye anawanenera Iwo. Eva anati. . . Satana anati kwa Eva, “Ine ndikudziwa Mulungu ananena Izo, koma Iwo kwenikweni sakutanthauza zimenezo. Iwo akutanthauza ichi.” Ndipo iye anazikhulupirira izo. Iye anazikhulupirira izo. Izo zinaswa umodzi, izo zinaswa chiyanjano, izo zinaswa mgwirizano, izo zinaswa dziko, izo zinaswa moyo, izo zinaswa chirichonse!

<sup>193</sup> Ndipo munthu amene samakhulupirira Mawu amodzi a Mawu a Mulungu, izo zimaswa chiyanjano chonsecho ndi zonse. Kulondola! Ife timawakhulupirira Iwo kapena ife sitimawakhulupirira Iwo. Tiyeni tikhale ndi Iwo! Mulungu ananena chomwecho, ndipo tiyeni tikhale ndi Iwo. Zinthu zambiri zomwe ine ndikuyenera kuzilumphaka apa, chifukwa nthawi yadutsa kale.

<sup>194</sup> Monga mu nthawi zakale, mu nthawi zakale pamene munthu achita izi, izo zinkabweretsa chiweruzo cha Mulungu ku dziko. Nsanja ya Babelo, mgwirizano wa ana a Kaini ndi ana a Seti, unabweretsa chiweruzo. Izo nthawizonse zimabweretsa chiweruzo cha Mulungu ku dziko lapansi. Mukuona? Oh, umodzi woona ndi Iye udzawuka mu chiweruzo, pamwamba pake, monga Nowa anachitira mu chiweruzo chija ndi banja lake. Nowa wolungamayo ndi banja lake anapita pamwamba pa ziweruzo. Kodi iwo anachita chiyani? Iwo anapita!

<sup>195</sup> M'bale Lee Vayle, ngati inu mungagwire ichi, ndi ichi apa. Limenero ndi funso lokhalo limene ife sitigwirizanapo, iye amakhulupirira kuti Mpingo udzadutsa mu chiweruzo. Ine sindimaziwona izo. Ine sindimazikhulupirira izo.

<sup>196</sup> Nowa sanadutse konse mu ziweruzo, iye anapita pamwamba pa ziweruzo. Abrahamu analibe moto nkomwe, iye anali kunja kwa motowo. Israeli sanali mu ziweruzo za Israeli, iye analekanitsidwa kuchoka ku moto, kunja kwa ziweruzo. Mpingo

udzakwera pamwamba pa chiweruzo, mu chombo cha Mzimu Woyera, udzawukitsidwa kuchoka pa dziko lapansi.

<sup>197</sup> Chinthu ichi cha Bungwe la Mpingo si chinanso mu dziko koma a—kutakasa kwa namwali wopusa, kuti adzasiyidwe kuno pa dziko lapansi kuti adzasankhe wotsutsakhristu. Koma Mpingo weniweni wa Mulungu udzayandama monga Nowa wokalamba anachitira, ndi kumapitirirabe kukalowa mu Ulemelero motsimikiza basi monga ine ndayimira pano. Ndi chifukwa chake Iye akuwasonkhanitsa iwo pamodzi. Ndicho chimene Liwulo likuyankhulabe lero. Ndicho chimene Mulungu akuchita, akusonkhanitsa mmodzi kuchokera ku Los Angeles, ndi mmodzi kuchokera ku Philadelphia, ndi mmodzi kuchokera ku Georgia, ndi zina zotero. Kuwasonkhanitsa iwo pamodzi, anthu Ake amene akulolera kuti akhulupirire Mawu a Mulungu wamoyo. “Monga mmene zinaliri mmasiku a Nowa, momwemonso izo zidzakhala pakudza kwa Mwana wa munthu, momwe owerengeka anapulumsidwa, basi owerengeka okha.” Chabwino, chombo chathu cha Mzimu Woyera chidzayandama pamwamba pa ziweruzo za Mulungu, chifukwa ife taweruzidwa kale, pamene ife tikumuvomereza Yesu, ndipo Iye anatenga chiweruzo chathu.

<sup>198</sup> Zipembedzo izi, ngakhalebe, ndi zosamva kwambiri! Izo ziri ngati Eva, iye ankafuna nzeru zake mosalabadira chimene Mawu a Mulungu anali. Nimrodi ankafuna nsanja yake, mosalabadira, Lemba kapena ayi! Iwo anali osamva! Eva ankadziwa bwinoko. Seti ankadziwa bwinoko kuposa kugwera akazi okongola amenewo. Israeli ankadziwa bwinoko kuposa kupita kunjira uko mu chigololo chimenecho. Chomwechonso inu! Koma ena ndi osamva kwambiri, Lemba kapena popanda Lemba! “Mulungu adalitsidwa, amayi anga anali Achipresbateria! Ine ndidzakhala, inenso.” Zipitirirani, zipitirirani ndi chinthu chokhacho chimene inu mungachite pamenepo. Mulungu achitire chifundo moyo wanu wochimwa. Inu mudzazithawa bwanji izo, pamene inu mukudziwa kuti izo ndi zooni? Ndipo ngati inu muwona Mawu a Mulungu, ndipo komabe osaganiza kuti Iwo ndi Choonadi, ndiye kuti pali chinachake cholakwika ndi kuzindikira kwauzimu kwanu. Ndiko kulondola ndendende. Tayang’anani kudutsa fukoli ndipo muwone kumene zinthu izi zikuchitika. Ife tiri pa nthawi yotsiriza, abwenzi. Kodi ife tangodutsa kumene mu Mibadwo ya Mpingo ndi kudziwa chimene chiti chichitike mu m’badwo wa Mpingo wa Laodikaya? Kodi ife sitinadutse kumene mu izo? Inu mukuwona chimene ine ndikutanthauza? Ife tiri pa nthawi yotsiriza.

<sup>199</sup> Mulungu akusonkhanitsa Osankhidwa kuchokera ku mphepo zinayi za dziko lapansi. Iye anati Iye adzatumiza angelo ndi kuwasonkhanitsa iwo. Nkulondola uko? Kuwasonkhanitsa iwo pamodzi, kuwalekanitsa iwo kwa namsongole. Amen. Namsongole adzawotchedwa, osati tirigu. Kulondola.

200 Koma, iwo ndi osamva kwambiri, iwo akhala nazo izo kapena ayi, sizipanga kusiyana kulikonse. Oh!

201 Koma Iwo osankhidwa a Mulungu akulamulidwa kuti atuluke kuchokera pakati pawo. “Khalani inu olekanitsidwa,” atero Mulungu, “ndipo Ine ndidzakulandirani inu. Musakhudze zinthu zawo zachidziko, ndipo Ine ndidzakhala Atate kwa inu, kapena Mulungu, ndipo inu mudzakhala ana Anga aamuna ndi aakazi. Musadzimangirize goli nokha ndi osakhulupirira, koma mutuluke mu zimenezo!” Mulungu akufuna kulekanitsidwa ndi dziko lapansi. Iye akufuna kuti akhale wolumikizidwa ndi inu, Iyemwini. Ndipo palibe dongosolo lopangidwa ndi munthu la bungwe, chipembedzo, kapena nthano zirizonse zopangidwa ndi munthu zomwe zidzayime konse. Izo zidzatengera Mulungu, Mzimu Woyera, mwa inu, kuti udzakulumikizitseni inu kwa Mulungu. Ndipo inu mudzadziwa bwanji kuti muli nawo Iwo? Mzimu Woyera umene unalemba Mawu udzachtira umboni Mawu aliwonse; ndipo zinthu zomwezo zimene Mzimu Woyera unachita mu Chipangano Chakale, Iye adzazichita mu Chipangano Chatsopano; azichita tsopano mofanana basi, chifukwa Yesu Khristu ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Ndipo inu simunamangidwe goli ndi mabungwe ndi dziko. Sindinu omangidwa goli ndi iwo. Musadzimange nokha goli pakati pawo, koma tulukani pakati pawo! Inu mwamangidwa goli kwa Khristu. Amen. Mwamangidwa goli kwa Ambuye Yesu Khristu.

202 Baibulo limati, mmasiku otsiriza kudzakhala mipingo, ngati nsanja ina ya Babulo. Iwo adzakhala nawo mawonekedwe aumulungu, ndi kukana Mawu a Mulungu ndi Mphamvu, Mphamvu ya Mawu Ake. Ndipo kodi Mawu ndi chiyani? Kodi Ufumu wa Mulungu ndi chiyani? Ife tikuyenera kukhala a Ufumu tisanakhale mzika za Mfumu. Ndi angati akudziwa zimenezo? Nenani “Ameni.” [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Chabwino, kodi inu mumalowa chotani mu Ufumu? Ufumu wa Mulungu ndi Mawu a Mulungu opangidwanso mu mphamvu. Amen. Opangidwa mphamvu; kuchotsa tchimo, kupereka zizindikiro. Chizindikiro chamtundu wanji? Ngati Iwo ali Mawu omwewo amene amatulutsa Mose, Iwo adzabweretsa chizindikiro chomwecho.

203 Chinthu chomwecho chimene chinamulekanitsa Loti wofunda. Tsopano, ife tikudziwa Loti anali wofunda, ndipo Yesu anati icho chidzakhala chizindikiro cha nthawi yotsiriza. Loti wofunda atakhala pamenepo, iye anali wachipembedzo, ndithudi, iye ndi mkazi wake. Ndipo iwo anali a mitundu yonse ya magulu, ndipo iye anali meya wa mzinda, ndipo, oh, apo panali zinthu zambiri zomwe zinkachitika. Iye anali wachipembedzo kwambiri. Iye amakhoza kuchereza alaliki ndi onse a iwo amene ankabwera, iye anali bwino mwanjira imeneyo. Koma, oh, m’bale, iye sanali Wosankhidwa ameneyo.

204 Tawonani chimene chinachitika! Bwanji? Mulungu yemweyo amene analekanitsa ndipo anabwera kwa Abrahamu ndi kumuwonetsa iye kutsimikizira kwa kulekanitsa kwake... Uhm! O Mulungu! Momwe ine ndikanafunira—ine ndikukhumba ndikanangochita chinachake kuti ndikuloleni inu muwone Icho. Mulungu anamuwonetsa Abrahamu, pokhala kuti iye anali atadzilekanitsa yekha, Iye anamuwonetsa iye kutsimikizira kwa izo, kuti Iye anali ndi iye ndipo pakati pake pomwe. Ndipo Yesu anati chinthu chomwecho chidzachitika mmasiku otsiriza. Osati fuko linali Abrahamu, iye anali mwa ochepa, koma Mulungu anali ndi iye. Iye anali atamulekanitsa iye nthawi imeneyo. Iye tikuyenera kudzilekanitsa tokha mmasiku otsiriza ano.

205 Ndipo ngati Mulungu anapereka chizindikiro kwa Mose, kwa Israeli, mneneri wodzozedwa, Lawi la Moto, anapereka chizindikiro kwa Abrahamu. Iye—Iye anapereka chizindikiro kwa Israeli. Iye anapereka chizindikiro kwa ophunzirawo. Chizindikiro chomwecho, nthawi iliyonse! Chizindikiro chomwecho, Lawi la Moto!

206 Paulo, pamene iye anali pa ulendo wake wopita ku Damasiko, apo panawala Lawi la Moto patsogolo pake, limene ngakhale linatulutsira maso ake kunja, linamugwetsera iye ku mawondo ake. Palibe wina aliyense analiwona Ilo. Aliyense anali atayima pamenepo, iwo sanaliwone Ilo. Ndipo Liwu linati, “Saulo, nchifukwa chiyani iwe ukundizunza Ine?”

207 Iye anati, “Ambuye, Inu ndinu Ndani?”

208 Iye anati, “Ndine Yesu.” Chizindikiro! Ndipo kodi iye anali chiyani? Mtumwi kwa Amitundu. Amen.

209 Ndife pano mu nthawi yotsiriza, kuchokera Kummawa ndi Kumadzulo, Kumpoto ndi Kummwera. Kodi ife tikuchita chiyani? Kukonzekera Mkwatulo umenewo. Kukonzekera ku... Kudzigwira tokha mokhazikika kwa maminiti pang’ono mpaka mnyewa uliwonse utadzazidwa ndi Mzimu Woyera. Kenako Iye adzakwera mmwamba. Oh, mai! Akuwaitanira anthu Ake pamodzi kwa Iyemwini, mu umodzi woona ndi Iyemwini, chifukwa ndi Mzimu Wake umodzi Woyera. “Mwa Mzimu umodzi ife tonse aliyense payekhapayekha timabatizidwa kulowa mu Thupi limodzi, palimodzi Thupi la Yesu Khristu.” Ndipo Yesu Khristu akukhala ndi Mzimu Wake mu thupi lathu, akuwutumikira Mpingo ndipo akuchita zinthu zomwezo zimene Iye ankachita, ngati a—ngati chizindikiro, ngati mbendera kwa dziko, kuti ife tiri mmasiku otsiriza, kukonzekera Mkwatulo. Oh, ine ndimamukonda Iye, sichoncho inu?

210 Ine ndikadali ndi bukhu apabe, koma sindingamapitirirenso, tikuchedwa kwambiri. Ndikhoza kudzalitenga ilo nthawi ina.

211 Iye tiri kumapeto. Umodzi. Kodi inu ndi mmodzi chotero ndi Mulungu? Umo ndi mmene inu mukuyenera kukhalira.

Eya. Ife tikuyenera kukhala mmodzi ndi Iye mpaka... Mulole malingaliro amene anali mwa Khristu akhale mwa inu. Zikatero Khristu, malingaliro Ake Omwe mwa inu adzazindikira Mawu aliwonse amene Iye anawalemba. Izo zinatero mwa atumwi, amagawaniza molondola Lemba, lomwe liri Choonadi, mwawona, Mzimu Woyera. Ngati Ichu chiri Choonadi, ndiye Iye adzachitira umboni za Ichu pobweretsa chizindikiro chomwecho chimene Iye anapereka kwa Mose, chizindikiro chomwecho chimene Iye anapereka kwa Abrahamu, chizindikiro chomwecho chimene Iye anachita ndi Khristu, chizindikiro chomwecho chimene Iye anachita ndi Paulo. Ife tiri mu nthawi yotsiriza. Iye ananena kuti izo zikanadzakhala. Ife tiri mu nthawi yakumapeto. Mpingo, pamodzi, ukusonkhana pamodzi mu mgwirizano, wina apa ndipo wina apo, kupanga izo.

<sup>212</sup> Iye anati, “Padzakhala awiri mmunda, Ine ndidzatenga mmodzi.” Mmodzi. Onani, “Awiri mmunda,” amenewo ndi masana, kukolola, “Ndidzatenga mmodzi ndipo ndidzasiya mmodzi. Padzakhala awiri pa bedi,” mbali ina ya dziko, “Ndidzamtenga mmodzi ndipo ndidzamsiya mmodzi,” pa kudza kwa Mwana wa munthu. Ndipo izo ndi zokhazikika kwambiri, ziri pafupi kwambiri.

<sup>213</sup> Musatero! Musatero, Adamu! Adamu! Eva, Adamu, ndiloleni ine ndifuwulire kwa inu, musadzamverenso bodza la mdierekezi. Khalani ndi Mawu a Mulungu, Ndi PAKUTI ATERO AMBUYE. Khalani ndi Mawu Ake. Kudzilekanitsa kwa Iwo ndi kuswa chiyanjano chanu ndi Mulungu, umodzi wa Mulungu mwa Mzimu Woyera. Ndiye ngati inu munena kuti muli ndi Mzimu Woyera ndipo izo sizikugwirizana ndi Mawu, ndiye inu sindinu aumodzi ndi Mulungu.

<sup>214</sup> Uwu ndi umodzi wa Mulungu, pamene inu...a—mzimu umene inu muli nawo ugwirizana ndi Mawu awa, ndi kumawonetsera Mawu awa ndi kuwapanga Mawu awa amphamvu kuti achite momwe Iwo ankachitira kumeneko.

<sup>215</sup> Tiyeni tinene izo pamodzi: “Umodzi ndi Mulungu ndi kukhala ndi Mzimu wa Mulungu mwa inu ukugwirizana ndi Mawu, Mawu onse, Mawu athunthu, ndi kumawapanga Iwo kuti aziwonetseredwa mu mphamvu.”

<sup>216</sup> Ndi zimenezotu, umenewo ndi umodzi ndi Mulungu. Pamene mphamvu imeneyo ikugwira ntchito mwa ine, ikugwira ntchito mwa inu, ndife amodzi. Amen! M’bale Kidd, pamene mphamvu ya Mzimu Woyera mwa ine ikugwira ntchito mwa inu, sipangakhale kusagwirizana, Mawu ali pamenepo. Iyo imagwira ntchito. Amen. Iyo imawapanga Iwo chimene Iwo ali, Mulungu wopangidwa thupi mwa inu mwa Mawu Ake. Mawu kupangidwa amphamvu pakati panu, Mawu aliwonse!

<sup>217</sup> Tsopano, kumbukirani, mdierekezi amatenga zochuluka zonse za Mawu amenewo, pafupifupi nainte-naini ndi nainte-

naini peresenti ya Iwo. Kahandirede ka nainte-naini ndi nainte-naini peresenti ya kahandirede kameneko, iye adzawapanga Iwo chimodzimodzi basi, komano iye adzalumphakuchoka *apa*, ndipo ameneyo ndi amene amayambitsa imfa pamenepo. Izo zimadula unyolo pakati pomwe, inu nkupita pansi.

<sup>218</sup> Mawu aliwonse! Kodi Yesu ananena chiyani? “Munthu sadzakhala moyo ndi mkate wokha, koma ndi Mawu aliwonse!” Osati mwa Mawu ochepa a Mulungu iye ati adzakhale moyo, osati mwa nainte-naini ndi nainte-naini peresenti ya Mawu a Mulungu. Koma ndi Mawu aliwonse amene atuluka mkamwa mwa Mulungu, munthu adzakhala moyo ndi Iwo.

<sup>219</sup> Satana anamutengera Iye pamwamba apo ndipo anati, “Kwalembedwa!” Mwaona, chimodzimodzi monga momwe iye ananenera kwa Eva, “Kwalembedwa! Kwalembedwa!”

Yesu anati, “Ndipo kwalembedwanso. . .”

<sup>220</sup> Iye anati, “Kwalembedwa, ‘Iye adzalamulira Angelo pa Inu.’ Baibulo linanena chomwecho!” Mnyamata, iye ndi wophunzira. “Kwalembedwa, ‘Iye adzalamulira Angelo Ake za Inu kuti Inu mungamenyetse phazi Lanu pa mwala, ndi kukunyamulani Inu mmwamba.’”

<sup>221</sup> Iye anati, “Kwalembedwanso, ‘Usamuyese Ambuye Mulungu wako.’”

<sup>222</sup> Iwo anati, “Ife tiri ndi Lemba,” Machitidwe 19, “ife tinabatizidwa ndi Yohane.”

<sup>223</sup> Paulo anali ndi chinthu chinachake, iye anati, “Izo sizigwiranso ntchito.” Mukuona? “Yohane ankangobatiza. . .” Iye sanali wosakhulupirira mawu a Yohane. Iye anati, “Ine ndikuuzani inu zomwe Yohane ananena. Yohane anati iye ankatiza ku kulapa, osati ku chikhululukiro cha machimo.” Nsembeyo inali isanaphedwe, mwaona. Iye anati, “Iye amabatiza ku kulapa, kunena kuti inu muzikhulupirira pa Iye amene anali nkudza.” Ndipo pamene iwo anamva ichi, iwo anabatizidwa mu Dzina la Ambuye wathu Yesu Khristu. Paulo anayika manja ake pa iwo odzazidwa kwambiri ndi Mawu, ndipo Mzimu Woyera unabwera pa iwo. Iwo anayamba kunenera, kuyankhula mmalirime, kumukweza Mulungu, ndipo ndi nthawi yotani! Oh, mai. Iwo unali mpingo waukulu bwanji? Thwelofu. Inde. Oh, Mulungu samachita mu manambala aakulu, Iye amachita mu mitima yowona. Tiyeni tikhale ndi mtima wotero. Kodi inu mumamukonda Iye? Tiyeni ife tipemphere.

<sup>224</sup> Oh, wokonedwa wanga woyendayenda, kodi iwe unayang’ana pa ana aakazi a Moabu kapena wawona ana aakazi (ine ndikuyankhula za mipingo) a Kaini? Momwe iwo asochelera kutali ndi Mawu! Kodi iwe, mzanga wofunika, kodi iwe wazindikira mmasiku otsiriza kuti zinthu izi zafika pochitika? Kodi mwakhala mukuzindikira posachedwapa za momwe Mawu a Mulungu akuwonetseredwa? Momwe kuti chitsitsimutso



chomwe chinamenyapo kamodzi chakhala chete, palibe zambiri zatsala? Icho ndi chiyani? Ndi bata mkuntho usanabwere. Ziweruzo zakonzeka. Kodi inu mwakhala mukuwonetsera zinthu izi? Kodi inu mwafanizitsa Lemba ndi Lemba, Mawu a Baibulo ndi Mawu a Baibulo, umboni ndi umboni? Kodi inu mwafanizitsa Mawu a Yesu amene Iye ananena kuti mdierekezi mmasiku otsiriza...zidzakhala pafupi kwambiri, ngati chinthu chenichenicho, mpaka ngati kukanakhala kotheka akanadzanyenga aliyense kupatula Osankhidwa, Mmodzi Wosankhidwayo. Tangoganizani, chiphunzitso cha Mwamalemba chimenecho chidzakhala chapafupi kwambiri! “Oh, ife timakhulupirira mu Mzimu Woyera, adalitsike Mulungu kwanthawizonse! Ife tiri nawo Mzimu Woyera, ife timayankhula mmalirime.” Ndipo kenako nkutembenuka ndi kuwakana Mawu? Eya. Mwaona, adzanyenga Osankhidwa omwe ngati nkotheka.

<sup>225</sup> Ngati alipo winawake muno amene sali bwino ndi Mulungu, ngati pali winawake pano amene akudwala kapena kusautsika...Pali mipango ndi zinthu ziri apa, ine ndizipempherera izo. Ine sindikusamala chomwe inu mukuchisowa. Lonjezo lililonse mu Bukhu ndi lanu. Ndi lanu.

<sup>226</sup> Tsopano, ine ndakubweretserani inu Mawu, kuwabweretsa Iwo kuchokera ku Genesis mpaka ku tsiku lino limene ife tikukhalamo, kumangogunda malo ndi kukuwonetsani inu. Malo mahandirede ambiri omwe ndikanagunda pambali pa izo, ine ndiribe nthawi. Koma ndithudi, mmenemo, inu mukhoza kuwona kuti zinthu za bungwe izi zachoka. Ndi lingaliro labodza la mdierekezi, kuyesera kumupanga bungwe munthu ndi umodzi wa malingaliro awo omwe ndi kuganiza. Pamene, ndi Mzimu Woyera umene ife timalumikizidwa kwa Mulungu ngati amodzi. Ndipo Mzimu Woyera umagwirizana ndi Mawu a Mulungu. Mwaona, Baibulo linati, Yesu ananena kuti iwo akanadzavomereza izo, inu mwaona, “Adzanyenga osankhidwa omwe ngati nkotheka.” Mukuona pamene ife tayima?

<sup>227</sup> Tsopano tengani Mawu a Mulungu awa mu dzanja la chikhulupiriro limenero. Kodi inu mukusowa chiyani mmawa uno? Inu mukusowa ubatizo wa madzi mu Dzina la Yesu Khristu? Dziwe ndilotsegula. Inu mukusowa ubatizo wa Mzimu Woyera? Iye akuyesera kukanikizira njira Yake mwa inu. Inu mukusowa machiritso? Bwanji, Mzimu Woyera Iyemwini, Mawu amene apangidwa mphamvu, ali pomwe pano tsopano, mphamvu kumene ya kuzindikira za mumtima ikuyang’ana pa omvetsera awa pano tsopano ndi kuwona Kuwala uko kukuzungulira ngati kuyaka. Kodi ine ndinayamba ndakuwuzanipo inu chirichonse cholakwika? [Osonkhana akuti, “Ayi.”—Mkonzi].

<sup>228</sup> Kodi ine ndinayambapo, monga—monga mneneri ananena kwa Israeli iwo asanazitengere mfumu yopangidwa ndi munthu, iye anati, “Kodi ine ndinayamba ndakuwuzanipo

inu chirichonse...? Kodi ine ndinayamba ndatengapo ndalama zanu? Kodi ine ndinabwerapo ndi kukupemphani inu ndalama ndi—ndi kumayendayenda nditakwera ndi kumakhala mnyumba zazikulu zapamwamba ndi kumanga zinthu zazikulu ndi kukutengerani ndalama zanu? Kodi ndinayamba ndakupemphanipo inu khobiri?”

“Ayi.”

<sup>229</sup> Kodi ine ndinayamba ndakuuzanipo inu chirichonse mu Dzina la Ambuye kupatula chimene Mulungu anadzachikwaniritsa? Kodi ine ndinayamba ndayankhulapo mu Dzina Lake koma chomwe icho chinali choncho? Kodi ine ndinayamba ndakuwuzanipo inu masomphenya pa omvetsera koma chimene kwenikweni chinali munthu amene anadzutsidwa, mlendo kapena chirichonse chimene iye angakhale, koma chimene iye ananena “Ndicho choonadi”? Kodi ine ndinayamba ndakuwuzanipo inu chirichonse cholakwika? [Osonkhana akuti, “Ayi.”—Mkonzi]. Ndiye ndiloleni ine ndikuwuzeni inu tsopano, PAKUTI ATERO AMBUYE, landirani Mzimu Woyera, Mzimu umene uti udzatenge Mawu a Mulungu mmanja amenewo a chikhulupiriro, kuwatulutsira kutali uko. Ufumu wonsewo ndi wanu. Ndi wanu, ana.

<sup>230</sup> Chifukwa chiyani inu mumabwera kuchokera ku Georgia, kuchokera ku dziko lonse, kuchokera ku Ohio, kuchokera ku Kansas, kulikonseko, chifukwa cha msonkhano wawung’ono? Ine ndikuganiza tepi yazimitsidwa tsopano, chotero, ine ndikhoza kunena izi. Mukuona? Chifukwa chiyani mumabwera monga chonchi? Nchiyani chimakupangitsani inu kuchita zimenezo? Ndi chiyani icho? Ine ndikuwawona anthu pano ochokera ku Arkansas, ochokera mailosi mahandirede kutali.

<sup>231</sup> Usiku watha, ndikubwera kuchokera ku Kansas City, m’bale wamng’ono wa Chipolishi atayima kumbuyo uko, anabwera, akutsogoleredwa, anati, “M’bale Branham, chiyambireni ine kumva za inu koyamba uko mu Canada zaka zambiri zapitazo, zinthu zimene inu munaziwona ndi kuzichita, ine ndazifufuza izo, mmbuyo ndi mtsogolo, mmwamba ndi pansu,” ndipo anati, “palibe chimodzi cha izo chimene chinayamba chakhala cholakwika.” Iye mwinamwake ndi Mkatolika wa Chipolishi, ndipo apa iye wabwera, akutenga matepi, akumapita uko ndi kumakawasewera iwo, akumakomanako ndi zolepheretsa. Atumiki amene akuyenera kukhala ndi ine ndi kumatithandizira ife, koma kumakana Mphamvu yake, kumakana Choonadi cha Mawu, ndi kumadzinenera kuti ali nawo Mzimu Woyera.

<sup>232</sup> Ine sindinadzitchulepo ndekha mneneri. Ndinu amene mumachita zimenezo. Koma, ngati ziri choncho, ndiye Mawu a Ambuye amachokera kuti? Kodi ife timadziwa bwanji ngati iwo ali owona kapena ayi pokhapokha ngati pali chinachake choti chiwaikire kumbuyo? Amenewo ndi Mawu

a Mulungu apa, Mawu olembedwa. Ndiyeno ngati Mawu olembedwa athandizidwa, ndiye kuti ndi Mulungu mu Mawu amenewo akupanga Mawu amenewo kukhala owona. Paulo anati, “Nditsatireni ine, monga ine ndikutsatira Khristu.”

<sup>233</sup> Tsopano, ngati inu muli ndi chosowa cha Mulungu cha matenda, cha chipulumutso, chiyani . . . kapena kuchotsa . . . Ena a inu akazi amene mulibe chisomo chokwanira kuti tsitsi lanu likule, ena a inu amuna omwe mulibe chisomo chokwanira kuti musiyeye kusuta ndudu, ena a inu alaliki omwe mulibe chisomo chokwanira kuti muvomereze choonadi cha ubatizo wa mmadzi mu Dzina la Yesu Khristu, ena a inu anthu odwala amene mukudwala ndipo mukudwala pafupi kufa, bwanji osatenga Mawu awa mmawa uno. Ine ndikuwuzani inu tsopano, Iwo ndi thupi pakati pathu! Atengereni Mawu amenewo mdzanja lanu.

<sup>234</sup> Apa papachikika chithunzi pakhoma, cha Mngelo wa Ambuye, Mmodzi yemwe uja amene ankatsogolera ana a Israeli, Mmodzi yemwe uja amene anakomana ndi Paulo, Mmodzi yemwe uja amene anali mwa Khristu. Ndipo Mzimu Woyera womwewo uli mwa inu, mwa inu, kukulumikizani inu ngati mmodzi. Nchiyani chimapangitsa mitima yathu kuyandikira pamodzi kwa mailosi mahandirede? Palibepo chinthu chonga icho mdziko. Iwo akubwera ku Mawu.

<sup>235</sup> “Pali kasupe wodzazidwa ndi Mwazi, wochokera mmitsempha ya Emanuele, kumene osakhulupirira amagwera pansu pa kusefukurako, ndipo amataya banga lonse la kulakwa kwawo. Chiyambireni mwa chikhulupiriro ine ndinawona mtsinje umenewo mabala Anu oyenderera amapereka, chikondi chowombola chakhala chiri nkhani yanga, ndipo chidzakhala mpaka ine ndidzafe.”

<sup>236</sup> Atate athu Akumwamba, apa pali mulu wa mipango, magolovesi, izo zikhoza kupita uko mu makalata. Ine sindikudziwa yemwe anayika izo apa, mwinamwake Billy, mwinamwake anthu muno mwa omvetsera. Ine ndikungomverera kuti ndichite ichi tsopano, Ambuye. Mulibe kalikonse mmanja mwanga, mulibe kalikonse mwa ine monga munthu. Sindinathe kudalira pa kumvetsetsa kwanga kwa umunthu. Sindikumvetsa chifukwa izi ziri choncho, koma ndikutsatira zomwe Inu munanena. “Iwo anatenga kuchokera pa thupi la Paulo, mipango ndi zovala, ndipo mizimu yoipa inatuluka mwa anthu.” Sizinali chifukwa chakuti iye anali munthu wamkulu, zinali chifukwa chakuti Mulungu anali ndi iye mu Mawu ndi mphamvu. Ndipo iye sanafunsire konse kwa atumwi, koma anapeza pamene iwo anadzakomana pamodzi kuti unali Uthenga womwewo, mtundu womwewo wa ubatizo, chimodzimodzi chirichonse chimene iwo ankachita, chinali diso kwa diso mofanana.

<sup>237</sup> Tsopano ine ndikupempha, Ambuye, chifukwa cha anthu

ofunika awa amene akukukhulupirirani Inu, kuti Inu muwachize iwo. Iwo mwa omvetsera, achizeni iwo, Ambuye. Mulole chikhulupiro chawo chingofikira mmwamba ndi kuwagwira Mawu amenewo pakali pano, ndi kuti, “Chotupa, matenda, choipa, iwe ukhoza kuchoka, ine ndikudula ndi Lupanga la Mulungu! Ine ndikukhulupirira! Chikhulupiro changa ndi champhamvu. Ndikukanikiza Lupanga mwakuya. Choka panjira yanga! Ine ndikudzuka pa mpando wanga, kuti ndikhale bwino.” “Ine ndikusanjika dzanja langa pa abambo anga, pa mlongo wanga, mwana wanga, pa woyandikana naye wanga. Ine ndikukhulupirira. Mawu Anu ndi Choonadi. Ine ndiri mu umodzi ndi Inu. Ntchito zomwe Inu munanena kuti Inu munazichita, ifenso tikanazichitanso. Ambuye Mulungu, ine ndikukhulupirira Mawu aliwonse. Ndipo ine ndikubwera patsogolo, ndikubwera patsogolo kudzatenga izo, kuti ndidzatenge izo mmawa uno.”

<sup>238</sup> O Mulungu, momwe ine ndimakhoza kuganizira pamene mpingo unali pa ulendo, pamene Mose anachita mantha pang’ono kumusi uko pa nyanja, iye anayamba kulirira kwa Ambuye. Ndipo Ambuye anati, “Ukulirira chiyani kwa Ine? Ukulirira chiyani kwa Ine? Yankhula ndipo upite patsogolo! Kodi Ine sindinakutume iwe ku ntchitoyo? Yankhula!” Kuyankhula chiyani? Mawu a Mulungu. “Iwo ali mwa iwe. Yankhula ndi kupita patsogolo. Usandilire Ine. Pita patsogolo.”

<sup>239</sup> Ndipo, Ambuye Mulungu, lero ine ndabwera mu Dzina la Ambuye Yesu. Ine ndabwera nditanamula Lupanga ili la chikhulupiro, kudzinenera umodzi wa Mulungu ndi munthu mwa Mzimu Woyera, kudzera mu zifundo ndi nsembe ya Yesu Khristu Mwana Wake. Ine ndikunyoza mdierekezi aliyense yemwe wamanga aliyense mu njira iliyonse mchhipinda chino, kaya ndi mnyamata kapena mtsikana, mwamuna kapena mkazi. Ine ndikunyoza matenda aliwonse. Ine ndikunyoza kukayikira kulikonse. Ine ndikunyoza mantha aliwonse. Ine ndikunyoza chirichonse chimene chiri chopanda umulungu, uwasiye omvetsera awa mu Dzina la Yesu Khristu! Tuluka mwa omvetsera awa, kuti ife tikhoze kukhala amodzi ndi Mulungu ndi kumutumikira Mulungu popanda matenda kapena mantha. Mulole mphamvu yomwe inatipanga ife kukhala amodzi ndi Mulungu. . . Mdierekezi ameneyo angakhoze bwanji kupanga phokoso mozungulira odzodzedwa? Mdierekezi ameneyo angayime bwanji kunja uko ndi kupanga phokoso ngati Goliati? Pamene Davide analowa mu msasa, ndipo anati, “Inu mukutanthauza kuti mukumulola Mfilisiti wosadulidwa uyo kuyima pamenepo ndi kumanyoza ankhondo a Mulungu wamoyo?”

<sup>240</sup> O Mulungu, apangeni amuna ndi akazi adzuke mu mphamvu ya Mzimu. Kulola wosatembenuka uyo, mdierekezi wokhumudwa uyo yemwe wavulaza mtundu wa anthu kudutsa

mu m'badwo, kuyima pano ndi kudzanyoza mpingo wa Mulungu wamoyo? Satana, tuluka, ndipo choka, mu Dzina la Yesu Khristu!

<sup>241</sup> Tsopano, inu amene muli ndi mphanvu zokwanira kuti munyamule Lupanga, tsopano poti muli ndi kumvetisa kokwanira mu Mawu a Mulungu kuti muwatenge Iwo kukhala chuma chanu, amene mungathe kutenga Mawu a Mulungu tsopano mdzanja lanu, kuwagwira Iwo mu dzanja la chikhulupiriro, ndi kuti, "Ine ndikutenga mbali yanga ndi Ambuye. Ine ndikhala umodzi ndi Mulungu wanga, kuyambira pano mpakana. Ine ndinyamula Lupanga ili la Mzimu mu Mawu awa, ndipo ine ndidzamudula mdierekezi ku lonjezo lirilonse limene Mulungu anandilonjeza ine."

<sup>242</sup> Ngati inu mukukhulupirira izo ndi mtima wanu wonse, ine ndikukupemphani inu ndiye mowona mtima ndi mtima wanga wonse, mu Dzina la Yesu Khristu, imani pa mapazi anu ndipo muvomereze izo. Kodi inu mukutanthauza izo? Kodi ndinu owona mtima? Kodi Mawu ali mdzanja lanu? Kodi dzanja lanu ndi chikhulupiriro chanu? Kwezani dzanja lanu lathupi kwa Mulungu, ndikuti, "Mulungu, mwa ichi, ndi dzanja langa lokwezedwa ndikulonjeza moyo wanga wonse. Ine ndikulonjeza solo yanga, ndikulonjeza kuganiza kwanga, ndikulonjeza zonse ku Mawu a Mulungu. Mulole Mzimu Woyera utenge chikhulupiriro changa tsopano ndi kundipatsa ine chinthucho. Mudulire kukayikira kulikonse kutali ndi ine. Ndipo, mwa chikhulupiriro, ine ndikulandira lonjezo limene ine ndapempha, mphindi ino."

<sup>243</sup> Ngati inu mukukhulupirira izo, nenani, "Ameni," tsopano. [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Nenani, "Ameni," kachiwiri. ["Ameni."] Amenii, amenii, amenii! Ndiye, ngati inu mukutanthauza izo ndi mtima wanu wonse, mu Dzina la Yesu Khristu, ine ndikukulonjezani inu zomwe inu munapempha. Amenii. Inu mukhulupirire izo ndi mtima wanu wonse. Mulungu akudalitseni inu.

M'bale Neville. 

62-0211 Umodzi  
Branham Tabernacle  
Jeffersonville, Indiana U.S.A.

CHICHEWA

©2024 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)